

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
<b>Mark 1</b>	<b>Mark 1</b>
1:1 Chiyambi chake cha Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu.	1:1 The beginning of the gospel of Jesus Christ, the Son of God;
1:2 Monga mwalembedwa mwa aneneri, Ona, ndituma mthenga wanga patsogolo pa nkhope yanu, amene adzakonza njira yanu.	1:2 As it is written in the prophets, Behold, I send my messenger before thy face, which shall prepare thy way before thee.
1:3 Mawu a wofuwula, m'chipululu, Konzani khwalala la Ambuye, lungamitsani njira zake.	1:3 The voice of one crying in the wilderness, Prepare ye the way of the Lord, make his paths straight.
1:4 Yohane anadza nabatiza m'chipululu, nalalikira ubatizo wa kutembenuka mtima woloza kuchikhulukiro cha machimo.	1:4 John did baptize in the wilderness, and preach the baptism of repentance for the remission of sins.
1:5 Ndipo adatuluka a ku dziko lonse la Yudeya, ndi a ku Yerusalemu onse; nadza kwa iye nabatizidwa ndi iye mumtsinje wa Yordano, powulula machimo awo.	1:5 And there went out unto him all the land of Judaea, and they of Jerusalem, and were all baptized of him in the river of Jordan, confessing their sins.
1:6 Ndipo Yohane amkabvala ubweya wangamila, ndi lamba lachikopa m'chuwuno mwake, nadya dzombe ndi uchi wa kuthengo.	1:6 And John was clothed with camel's hair, and with a girdle of a skin about his loins; and he did eat locusts and wild honey;
1:7 Ndipo adalalikira kuti, Wondipambana ine mphamvu akudza pambuyo panga, sindiyenera kuwerama kumasula lamba la nsapato zake ine.	1:7 And preached, saying, There cometh one mightier than I after me, the latchet of whose shoes I am not worthy to stoop down and unloose.
1:8 Ine zowonadi ndakubatzani inu ndi madzi; koma Iye adzakubatzani ndi Mzimu Woyera.	1:8 I indeed have baptized you with water: but he shall baptize you with the Holy Ghost.
1:9 Ndipo kudali masiku omwewo, Yesu anadza kuchokera ku Nazarete wa ku Galileya, nabatizidwa ndi Yohane m'Yordano.	1:9 And it came to pass in those days, that Jesus came from Nazareth of Galilee, and was baptized of John in Jordan.
1:10 Ndipo pomwepo, potuluka m'madzi, adawona Iye thambo litatseguka ndipo Mzimu adatsikira pa Iye monga nkhunda:	1:10 And straightway coming up out of the water, he saw the heavens opened, and the Spirit like a dove descending upon him:
1:11 Ndipo mawu adatuluka kumwamba, wonena, Uyu ndiye Mwana wanga wokonedwa , mwa Iyeyu ndikondwera bwino.	1:11 And there came a voice from heaven, saying, Thou art my beloved Son, in whom I am well pleased.
1:12 Ndipo pomwepo Mzimu udampititsa Iye kuchipululu.	1:12 And immediately the spirit driveth him into the wilderness.
1:13 Ndipo adakhala m'chipululu masiku makumi anayi nayesedwa ndi Satana; nakhala ndi zirombo, ndipo angelo adamtumikira Iye.	1:13 And he was there in the wilderness forty days, tempted of Satan; and was with the wild beasts; and the angels ministered unto him.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
1:14 Tsopano atatha kuperekedwa Yohane mundende, Yesu anadza ku Galileya, nalalikira Uthenga Wabwino wa Mulungu,	1:14 Now after that John was put in prison, Jesus came into Galilee, preaching the gospel of the kingdom of God,
1:15 Nanena, nthawi yakwanira ndipo Ufumu wa Mulungu wayandikira; lapani, khulupirirani Uthenga Wabwino.	1:15 And saying, The time is fulfilled, and the kingdom of God is at hand: repent ye, and believe the gospel.
1:16 Ndipo pakuyenda m’mbali mwa nyanja ya galileya, adawona Simoni ndi Andreyo, mbale wake, alimkuponya khoka m’nyanja; pakuti adali asodzi.	1:16 Now as he walked by the sea of Galilee, he saw Simon and Andrew his brother casting a net into the sea: for they were fishers.
1:17 Ndipo Yesu adanena nawo, Idzani pambuyo panga, ndipo ndidzakusandutsani inu asodzi a anthu	1:17 And Jesus said unto them, Come ye after me, and I will make you to become fishers of men.
1:18 Ndipo pomwepo adasiya makoka awo, namtsata Iye.	1:18 And straightway they forsook their nets, and followed him.
1:19 Ndipo atapita patsogolo pang’ono, adawona Yakobo, mwana wa Zebedayo, ndi Yohane mbale wake, iwonso adali m’chombo ali kusoka makoka awo:	1:19 And when he had gone a little farther thence, he saw James the son of Zebedee, and John his brother, who also were in the ship mending their nets.
1:20 Ndipo pomwepo adawayitana iwo; ndipo adasiya atate wawo Zebedayo m’chombomo pamodzi ndi antchito wolembedwa, namtsata Iye.	1:20 And straightway he called them: and they left their father Zebedee in the ship with the hired servants, and went after him.
1:21 Ndipo iwo adalowa m’Kapernawo; ndipo pomwepo pa tsiku la sabata Iye adalowa m’sunagoge naphunzitsa.	1:21 And they went into Capernaum; and straightway on the sabbath day he entered into the synagogue, and taught.
1:22 Ndipo adazizwa ndi chiphunzitso chake; pakuti adaphunzitsa monga mwini mphamvu, simonga alembi.	1:22 And they were astonished at his doctrine: for he taught them as one that had authority, and not as the scribes.
1:23 Ndipo pomwepo padali munthu m’sunagoge mwawo adali ndi mzimu wonyansa; ndipo adafuwula iye,	1:23 And there was in their synagogue a man with an unclean spirit; and he cried out,
1:24 Kuti, Tisiyeni, tiri ndi chiyani ife ndi Inu Yesu wa ku Nazarete? Kodi mwadza kudzatiwononga ife? Ndikudziwani, ndinu Woyerayo wa Mulungu.	1:24 Saying, Let us alone; what have we to do with thee, thou Jesus of Nazareth? art thou come to destroy us? I know thee who thou art, the Holy One of God.
1:25 Ndipo Yesu adawudzudzula, kuti, Khala chete, nutuluke mwa iye. Free Bibles: <a href="http://freebiblegospeltoallnations.blogspot.com">http://freebiblegospeltoallnations.blogspot.com</a> 48 Chewa Holy Bible - New Testament	1:25 And Jesus rebuked him, saying, Hold thy peace, and come out of him.
1:26 Ndipo pamene mzimu wonyansa, pom’ng’amba iye ndi kufuwula ndi mawu akulu, udatuluka mwa iye.	1:26 And when the unclean spirit had torn him, and cried with a loud voice, he came out of him.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
1:27 Ndipo adazizwa onse, kotero kuti adafunsana mwa iwo okha, kuti, Ichi nchiyani? Chiphunzitso chatsopano! Ndi mphamvu Iye alamula ngakhale mizimu yonyansa, ndipo idamvera Iye.	1:27 And they were all amazed, insomuch that they questioned among themselves, saying, What thing is this? what new doctrine is this? for with authority commandeth he even the unclean spirits, and they do obey him.
1:28 Ndipo kutchuka kwake kudabuka pompaja ku dziko lonse la Galileya lozungulurapo.	1:28 And immediately his fame spread abroad throughout all the region round about Galilee.
1:29 Ndipo pomwepo, potuluka m’sunagoge, iwo adalowa m’nyumba ya Simoni ndi Andreyana pamodzi ndi Yakobo ndi Yohane.	1:29 And forthwith, when they were come out of the synagogue, they entered into the house of Simon and Andrew, with James and John.
1:30 Ndipo mayi wake amkazi wa Simoni adali gone wodwala malungo; ndipo pomwepo adamuwuza za iye!	1:30 But Simon's wife's mother lay sick of a fever, and anon they tell him of her.
1:31 Ndipo anadza namgwira Iye pa dzanja, namuwutsa; ndipo nthawi yomweyo malungo adamleka, ndipo adawatumikira iwo.	1:31 And he came and took her by the hand, and lifted her up; and immediately the fever left her, and she ministered unto them.
1:32 Ndipo madzulo, litalowa dzuwa, anadza nawo kwa Iye onse wodwala, ndi wogwidwa ndi ziwanda.	1:32 And at even, when the sun did set, they brought unto him all that were diseased, and them that were possessed with devils.
1:33 Ndipo mzinda wonse udasonkhana pakhomo	1:33 And all the city was gathered together at the door.
1:34 Ndipo adachiritsa anthu ambiri wodwala nthenda za mitundu mitundu, natulutsa ziwanda zambiri; ndipo sadalole ziwandazo kuyankhula, chifukwa zidamdziwa Iye.	1:34 And he healed many that were sick of divers diseases, and cast out many devils; and suffered not the devils to speak, because they knew him.
1:35 Ndipo m’mawa mwake adawuka usikusiku, natuluka napita pa yekha, napemphera kumeneko.	1:35 And in the morning, rising up a great while before day, he went out, and departed into a solitary place, and there prayed.
1:36 Ndipo Simoni ndi amzake adali naye, adamsata Iye.	1:36 And Simon and they that were with him followed after him.
1:37 Ndipo pamene adampeza Iye, adanena naye, Akufunani Inu anthu onse.	1:37 And when they had found him, they said unto him, All men seek for thee.
1:38 Ndipo adanena kwa iwo, Tiyeni kwina, ku mizinda ili pafupi apa, kuti ndikalalikire komweko; pakuti ndadzera ntchito imeneyi.	1:38 And he said unto them, Let us go into the next towns, that I may preach there also: for therefore came I forth.
1:39 Ndipo adalowa m’masunagoge mwawo m’Galileya monse, nalalikira, natulutsa ziwanda.	1:39 And he preached in their synagogues throughout all Galilee, and cast out devils.
1:40 Ndipo adadza kwa Iye wodwala khate, nampempha Iye, namgwadira Iye, ndi kunena ndi Iye. Ngati mufuna mukhoza kundikonza.	1:40 And there came a leper to him, beseeching him, and kneeling down to him, and saying unto him, If thou wilt, thou canst make me clean.

<p><b>NYANJA</b></p>	<p><b>NEW INTERNATIONAL VERSION</b></p>
<p>1:41 Ndipo Yesu adagwidwa chifundo, natambasula dzanja lake namkhudza iye, nanena naye, Ndifuna; khala wokonzedwa.</p>	<p>1:41 And Jesus, moved with compassion, put forth his hand, and touched him, and saith unto him, I will; be thou clean.</p>
<p>1:42 Ndipo atangoyankhula nthawi yomweyo, khate lidamchoka, ndipo adakonzedwa.</p>	<p>1:42 And as soon as he had spoken, immediately the leprosy departed from him, and he was cleansed.</p>
<p>1:43 Ndipo adamulamulira iye, namtulutsa pomwepo;</p>	<p>1:43 And he straitly charged him, and forthwith sent him away;</p>
<p>1:44 Ndipo adanena kwa iye, Ona, usati unene kanthu kwa munthu aliyense; koma pita, ukadziwonetse wekha kwa wansembe, nuperekepo makonzedwe ako zimene adalamulira Mose, zikhale mboni kwa iwo</p>	<p>1:44 And saith unto him, See thou say nothing to any man: but go thy way, shew thyself to the priest, and offer for thy cleansing those things which Moses commanded, for a testimony unto them.</p>
<p>1:45 Ndipo iye adatuluka nayamba kulengeza ndithu, ndi kubukitsa nkhaniyo, kotero kuti Yesu sadakhoze kulowanso poyera mu mzinda, koma adakhala padera m'zipululu; ndipo anadza kwa Iye anthu wochokera ku madera onse.</p>	<p>1:45 But he went out, and began to publish it much, and to blaze abroad the matter, insomuch that Jesus could no more openly enter into the city, but was without in desert places: and they came to him from every quarter.</p>
<p><b>Mark 2</b></p>	<p><b>Mark 2</b></p>
<p>2:1 Ndipo Iye adalowanso m'Kapernawo atapita masiku ena, ndipo kudamveka kuti adali m'nyumba.</p>	<p>2:1 And again he entered into Capernaum after some days; and it was noised that he was in the house.</p>
<p>2:2 Ndipo ambiri adasonkhana pamodzi, kotero kuti adasowa malo wowalandirirapo, ngakhale pakhomu pomwe. Ndipo adawalalikira iwo mawu.</p>	<p>2:2 And straightway many were gathered together, insomuch that there was no room to receive them, no, not so much as about the door: and he preached the word unto them.</p>
<p>2:3 Ndipo anadza kwa Iye wotenga munthu wodwala manjenje, wonyamulidwa ndi anthu anayi.</p>	<p>2:3 And they come unto him, bringing one sick of the palsy, which was borne of four.</p>
<p>2:4 Ndipo pamene sadakhoze kufika kudali Iye, chifukwa cha khamu la anthu, adasasula denga pokhala Iye; ndipo pamene adatha kulibowola adatsitsa kama amene wodwala manjenjeyo adagona.</p>	<p>4 And when they could not come nigh unto him for the press, they uncovered the roof where he was: and when they had broken it up, they let down the bed wherein the sick of the palsy lay.</p>
<p>2:5 Pamene Yesu adawona chikhulupiriro chawo, adanena kwa wodwala manjenjeyo, Mwana, machimo ako akhululukidwa.</p>	<p>2:5 When Jesus saw their faith, he said unto the sick of the palsy, Son, thy sins be forgiven thee.</p>
<p>2:6 Koma adakhalapo ena alembi pamenepo amene adaganizira mumtima mwawo,</p>	<p>2:6 But there was certain of the scribes sitting there, and reasoning in their hearts,</p>

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
2:7 Kodi n’chifukwa chiyani munthu ameneyu akuchitira Mulungu mwano wotere? Akhoza ndani kukhululukira machimo, koma m’modzi, ndiye Mulungu?	2:7 Why doth this man thus speak blasphemies? who can forgive sins but God only?
2:8 Ndipo pomwepo Yesu pozindikira mu mzimu wake kuti alikuganizira chomwecho mwa iwo okha, adanena nawo, Muganiza bwanji zinthu izi m’mitima yanu?	2:8 And immediately when Jesus perceived in his spirit that they so reasoned within themselves, he said unto them, Why reason ye these things in your hearts?
2:9 Chapafupi n’chiti, kapena kumuwuza wodwala manjenje kuti, Machimo ako akhululukidwa; kapena kuti, Nyamuka, senza mphasa yako, nuyende?	2:9 Whether is it easier to say to the sick of the palsy, Thy sins be forgiven thee; or to say, Arise, and take up thy bed, and walk?
2:10 Koma kuti mudziwe kuti Mwana wa munthu ali nazo mphamvu zakukhululukira machimo pa dziko lapansi (adanena ndi wodwala manjenjeyo,)	2:10 But that ye may know that the Son of man hath power on earth to forgive sins, (he saith to the sick of the palsy,)
2:11 Ndikuwuzwa iwe, Nyamuka, senza mphasa yako, numuke kwanu.	2:11 I say unto thee, Arise, and take up thy bed, and go thy way into thine house.
2:12 Ndipo pomwepo adanyamuka iye, nasenza mphasa, natuluka pamaso pa iwo onse; koterokuti anadabwa onse, nalemekeza Mulungu, nanena kuti, zotere sitidaziwonepo ndi kale lonse.	2:12 And immediately he arose, took up the bed, and went forth before them all; insomuch that they were all amazed, and glorified God, saying, We never saw it on this fashion.
2:13 Ndipo adatulukanso kumka m’mbali mwa nyanja; ndipo linadza kwa Iye khamu lonse la anthu, ndipo adawaphunzitsa.	2:13 And he went forth again by the sea side; and all the multitude resorted unto him, and he taught them.
2:14 Ndipo popita adawona Levi mwana wa Alifeyo atakhala polandirira msonkho, ndipo adanena naye, Tsata Ine, ndipo adanyamuka namtsata Iye.	2:14 And as he passed by, he saw Levi the son of Alphaeus sitting at the receipt of custom, and said unto him, Follow me. And he arose and followed him.
2:15 Ndipo kudali kuti Yesu atakhala pachakudya m’nyumba mwake, ndipo amisonkho, ndi wochimwa ambiri adakhala pansipamodzi ndi Yesu ndi wophunzira ake, pakuti adali ambiri, ndipo adamtsata Iye.	2:15 And it came to pass, that, as Jesus sat at meat in his house, many publicans and sinners sat also together with Jesus and his disciples: for there were many, and they followed him.
2:16 Ndipo pamene Alembi ndi Afarisi adawona Iye kuti alimkudya nawo wochimwa ndi amisonkho, adanena ndi wophunzira ake, Uyu akudya ndi kumwa nawo amisonkho ndi wochimwa?	2:16 And when the scribes and Pharisees saw him eat with publicans and sinners, they said unto his disciples, How is it that he eateth and drinketh with publicans and sinners?
2:17 Ndipo pamene Yesu adamva ichi, adanena nawo, Wolimba safuna sing’anga, koma wodwala ndiwo; sindidadza kudzayitana wolungama, koma wochimwa kuti alape.	2:17 When Jesus heard it, he saith unto them, They that are whole have no need of the physician, but they that are sick: I came not to call the righteous, but sinners to repentance.

<p><b>NYANJA</b></p>	<p><b>NEW INTERNATIONAL VERSION</b></p>
<p>2:18 Ndipo wophunzira a Yohane ndi Afarisi adalimkusala kudya; ndipo anadza, nanena ndi Iye, Bwanji asala kudya wophunzira a Yohane, ndi wophunzira Afarisi, koma wophunzira anu sasala kudya?</p>	<p>2:18 And the disciples of John and of the Pharisees used to fast: and they come and say unto him, Why do the disciples of John and of the Pharisees fast, but thy disciples fast not?</p>
<p>2:19 Ndipo Yesu adanena nawo, Kodi akhoza kusala kudya ana a ukwati pamene mkwati ali pamodzi nawo? Pokhala ali naye mkwati pamodzi ndi iwo sakhoza kusala.</p>	<p>2:19 And Jesus said unto them, Can the children of the bridechamber fast, while the bridegroom is with them? as long as they have the bridegroom with them, they cannot fast.</p>
<p>2:20 Koma adzafika masiku, pamene mkwati adzachotsedwa kwa iwo, ndipo pamenepo adzasala kudya m`masiku amenewo.</p>	<p>2:20 But the days will come, when the bridegroom shall be taken away from them, and then shall they fast in those days.</p>
<p>2:21 Palibe munthu asokerera chigamba cha nsalu yatsopano pa chobvala chakale; mwina chigamba chatsopanocho chikhoza kuzomoka kuyakaleyo, ndipo chibowo chake chikhala chachikulu.</p>	<p>2:21 No man also seweth a piece of new cloth on an old garment: else the new piece that filled it up taketh away from the old, and the rent is made worse.</p>
<p>2:22 Ndipo palibe munthu amathira vinyo watsopano m`mabotolo akale; pena vinyo adzaswa mabotolo, ndipo akhoza kuwonongeka vinyo, ndi mabotolo omwe; koma vinyo watsopano, amathiridwa m`mabotolo atsopano.</p>	<p>2:22 And no man putteth new wine into old bottles: else the new wine doth burst the bottles, and the wine is spilled, and the bottles will be marred: but new wine must be put into new bottles.</p>
<p>2:23 Ndipo kunali kuti adapita Iye pakati pa minda ya tirigu tsiku la sabata; ndipo wophunzira ake poyenda adayamba kubudula ngala za tirigu.</p>	<p>2:23 And it came to pass, that he went through the corn fields on the sabbath day; and his disciples began, as they went, to pluck the ears of corn.</p>
<p>2:24 Ndipo Afarisi adanena kwa Iye, Tawonani, achitiranj chosaloleka kuchitika tsiku la sabata?</p>	<p>2:24 And the Pharisees said unto him, Behold, why do they on the sabbath day that which is not lawful?</p>
<p>2:25 Ndipo adanena nawo, simudawerenga konse chimene adachichita Davide, pamene adasowa, namva njala, iye ndi iwo amene adali pamodzi naye?</p>	<p>2:25 And he said unto them, Have ye never read what David did, when he had need, and was an hungred, he, and they that were with him?</p>
<p>2:26 Kutu adalowa m`nyumba ya Mulungu masiku a Abyatara, mkulu wa ansembe, ndipo anadya mikate yowonetsera yosaloleka kudya ena, koma ansembe okha, ndipo adawapatsanso iwo amene adali naye?</p>	<p>2:26 How he went into the house of God in the days of Abiathar the high priest, and did eat the shewbread, which is not lawful to eat but for the priests, and gave also to them which were with him?</p>
<p>2:27 Ndipo adanena kwa iwo, sabata lidayikidwa chifukwa cha munthu, si munthu chifukwa cha sabata:</p>	<p>2:27 And he said unto them, The sabbath was made for man, and not man for the sabbath:</p>
<p>2:28 Motero Mwana wa munthu ali Mbuye wa Sabata</p>	<p>2:28 Therefore the Son of man is Lord also of the sabbath.</p>

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
<b>Mark 3</b>	<b>Mark 3</b>
3:1 Ndipo adalowanso m’sunagoge; ndipo mudali munthu m’menemo adali ndi dzanja lake lopuwala.	3:1 And he entered again into the synagogue; and there was a man there which had a withered hand.
3:2 Ndipo adamuyang’anira Iye ngati adzamchiritsa iye tsiku la sabata; kuti amtsutse Iye.	3:2 And they watched him, whether he would heal him on the sabbath day; that they might accuse him.
3:3 Ndipo Iye adanena ndi munthu adali ndi dzanja lopuwala, Tayimilira.	3:3 And he saith unto the man which had the withered hand, Stand forth.
3:4 Ndipo adanena kwa iwo, N’kololedwa tsiku la sabata kuchita zabwino, kapena zoyipa? Kupulumutsa moyo kapena kupha? Koma adakhala chete.	3:4 And he saith unto them, Is it lawful to do good on the sabbath days, or to do evil? to save life, or to kill? But they held their peace.
3:5 Ndipo m’mene adawawunguza ndi mkwiyo, ndi kumva chisoni chifukwa cha kuwuma kwa mitima yawo, adanena kwa munthuyo, Tambasula dzanja lako. Ndipo adalitambasula; ndipo lidachira dzanja monga limzake.	3:5 And when he had looked round about on them with anger, being grieved for the hardness of their hearts, he saith unto the man, Stretch forth thine hand. And he stretched it out: and his hand was restored whole as the other.
3:6 Ndipo Afarisi adatuluka, ndipo pomwepo adamkhalira upo ndi Aherode monga momwe angamuwonongere Iye.	3:6 And the Pharisees went forth, and straightway took counsel with the Herodians against him, how they might destroy him.
3:7 Ndipo Yesu adachokako pamodzi ndi wophunzira ake namka kunyanja; ndipo lidamtsata khamu lalikulu la a ku Galileya, ndi la aku Yudeya,	3:7 But Jesus withdrew himself with his disciples to the sea: and a great multitude from Galilee followed him, and from Judaea,
3:8 Ndi wochokera ku Yerusalemu, ndi a ku Idumeya, ndi a ku tsidya lina la Yordano, ndi a kufupi ku Turo ndi Sidoni, khamu lalikulu, pakumva zazikuluzo adazichita, linadza kwa Iye.	3:8 And from Jerusalem, and from Idumaea, and from beyond Jordan; and they about Tyre and Sidon, a great multitude, when they had heard what great things he did, came unto him.
3:9 Ndipo adayankhula kwa wophunzira ake, kuti chombo chaching’ono chidikire Iye, chifukwa cha khamulo, kuti angamkanikize Iye.	3:9 And he spake to his disciples, that a small ship should wait on him because of the multitude, lest they should throng him.
3:10 Pakuti adawachiritsa ambiri; kotero kuti onse wokhala nayo miliri adamkanikiza Iye, kuti akamkhudze,	3:10 For he had healed many; insomuch that they pressed upon him for to touch him, as many as had plagues.
3:11 Ndipo mizimu yonyansa, m’mene idamuwona Iye, idagwa pansu pamaso pake, nifuwula, niyiti, Inu ndinu Mwana wa Mulungu.	3:11 And unclean spirits, when they saw him, fell down before him, and cried, saying, Thou art the Son of God.
3:12 Ndipo pomwepo Iye adayilamulira kuti isamuwulule Iye.	3:12 And he straitly charged them that they should not make him known.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
3:13 Ndipo Iye adakwera m’phiri, nadziyitanira iwo amene adawafuna Iye mwini; ndipo anadza kwa Iye.	3:13 And he goeth up into a mountain, and calleth unto him whom he would: and they came unto him.
3:14 Ndipo adasanjika manja pa khumi ndi awiri kuti akhale ndi Iye, ndi kuti akawatume kukalalikira.	3:14 And he ordained twelve, that they should be with him, and that he might send them forth to preach,
3:15 Ndi kuti akhale nazo mphamvu zochiritisa ndi zotulutsa ziwanda.	3:15 And to have power to heal sicknesses, and to cast out devils:
3:16 Ndipo Simoni adamutcha Petro.	3:16 And Simon he surnamed Peter;
3:17 Ndi Yakobo mwana wa Zebedeyo, ndi Yohane m’bale wake wa Yakobo, iwo adawatcha Boanerge, ndiko kuti Ana a bingu;	3:17 And James the son of Zebedee, and John the brother of James; and he surnamed them Boanerges, which is, The sons of thunder:
3:18 Ndi Andreyo, ndi Filipo ndi Bartolomeyo, ndi Mateyu, ndi Tomasi ndi Yakobo mwana waAlifeyo, ndi Tadeyo, ndi Simoni Mkanani,	3:18 And Andrew, and Philip, and Bartholomew, and Matthew, and Thomas, and James the son of Alphaeus, and Thaddaeus, and Simon the Canaanite,
3:19 Ndi Yudase Isikariyote, ndiye amene adampereka Iye. Ndipo adalowa m’nyumba.	3:19 And Judas Iscariot, which also betrayed him: and they went into an house.
3:20 Ndipo khamulo lidasonkhananso, kotero kuti sadadye iwo konse mkate.	3:20 And the multitude cometh together again, so that they could not so much as eat bread.
3:21 Ndipo pamene abwenzi ake adamva adadza kudzamgwira Iye; pakuti adati adayaluka.	3:21 And when his friends heard of it, they went out to lay hold on him: for they said, He is beside himself.
3:22 Ndipo alembi amene adatsika kuchokera ku Yerusalemu adati, Ali ndi Belizebule, ndipo ndi mkulu wawo wa ziwanda atulutsa ziwanda.	3:22 And the scribes which came down from Jerusalem said, He hath Beelzebub, and by the prince of the devils casteth he out devils.
3:23 Ndipo adawayitana iwo, nanena nawo m’mafanizo, Satana angathe bwanji kutulutsa Satana?	3:23 And he called them unto him, and said unto them in parables, How can Satan cast out Satan?
3:24 Ndipo ufumu ukagawanika pa wokha, sukhoza kukhazikika.	3:24 And if a kingdom be divided against itself, that kingdom cannot stand.
3:25 Ndipo ngati nyumba igawanika pa iyo yokha, siyikhoza kukhazikika nyumbayo payokha.	3:25 And if a house be divided against itself, that house cannot stand.
3:26 Ndipo ngati Satana adziwukira mwini yekha, nagawanika sakhoza kuyima payekha, koma atsirizika.	3:26 And if Satan rise up against himself, and be divided, he cannot stand, but hath an end.



NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
3:27 Palibe munthu akhoza kulowa m'nyumba ya munthu wa mphamvu, ndi kuwononga katundu wake, koma ayambe wamanga munthu wa mphamvuyo; ndipo pamenepo adzawononga za m'nyumba mwake.	3:27 No man can enter into a strong man's house, and spoil his goods, except he will first bind the strong man; and then he will spoil his house.
3:28 Indetu, ndinena ndi inu, Machimo onse ana anthu, ndi zamwano zili zonse adzachita adzakhulukidwa,	3:28 Verily I say unto you, All sins shall be forgiven unto the sons of men, and blasphemies wherewith soever they shall blaspheme:
3:29 Koma ali yense amene adzachitira Mzimu Woyera mwano alibe kukhulukidwa nthawi yonse, koma ali m'chiweruziro chowopsa chosantha;	3:29 But he that shall blaspheme against the Holy Ghost hath never forgiveness, but is in danger of eternal damnation.
3:30 Chifukwa adanena, Ali ndi mzimu wonyansa.	3:30 Because they said, He hath an unclean spirit.
3:31 Ndipo anadza amake ndi abale ake, nayima kunja, namtumizira uthenga kumuyitana.	3:31 There came then his brethren and his mother, and, standing without, sent unto him, calling him.
3:32 Ndipo khamu lambiri lidakhala pansi momzungulira; nanena kwa Iye, Onani, amayi anu ndi abale anu ali kunja akukufunani Inu.	3:32 And the multitude sat about him, and they said unto him, Behold, thy mother and thy brethren without seek for thee.
3:33 Ndipo adawayankha iwo nanena, Amayi wanga ndi abale anga ndani?	3:33 And he answered them, saying, Who is my mother, or my brethren?
3:34 Ndipo adawunguza wunguza iwo amene adakhala momzungulira Iye, nanena, Tawonani, amayi wanga ndi abale anga.	3:34 And he looked round about on them which sat about him, and said, Behold my mother and my brethren!
3:35 Pakuti ali yense adzachita chifuniro cha Mulungu, yemweyo ndiye mbale wanga ndi mlongo, ndi amayi.	3:35 For whosoever shall do the will of God, the same is my brother, and my sister, and mother.
<b>Mark 4</b>	<b>Mark 4</b>
4:1 Ndipo adayambanso kuphunzitsa pambali pa nyanja. Ndipo adasonkhana kwa Iye khamu lalikulukulu, kotero kuti adalowa Iye m'chombo, nakhala m'nyanja; ndipo khamu lonse lidakhala pamtunda m'bali mwa nyanja.	4:1 And he began again to teach by the sea side: and there was gathered unto him a great multitude, so that he entered into a ship, and sat in the sea; and the whole multitude was by the sea on the land.
4:2 Ndipo adawaphunzitsa zinthu zambiri m'mafanizo, nanena nawo m'chiphunzitso chake,	4:2 And he taught them many things by parables, and said unto them in his doctrine,
4:3 Mverani; Tawonani, wofesa adatuluka kukafesa:	4:3 Hearken; Behold, there went out a sower to sow:
4:4 Ndipo kudali, zitapita izi pamene amkafesa, zina zidagwa m'mbali mwa njira ndi mbalame zamumlengalenga zinadza ndi kuzidya.	4:4 And it came to pass, as he sowed, some fell by the way side, and the fowls of the air came and devoured it up.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
4:5 Ndipo zina zinagwa pa nthaka ya mwala pamene panalibe dothi lambiri, ndipo pomwepo zidamera, koma zinalibe dothi lakuya:	4:5 And some fell on stony ground, where it had not much earth; and immediately it sprang up, because it had no depth of earth:
4:6 Ndipo pamene dzuwa lidakwera zidapsereera; ndipo popeza zidalibe mizu zidafota	4:6 But when the sun was up, it was scorched; and because it had no root, it withered away.
4:7 Ndipo zina zinagwa pakati pa minga, ndipo minga idakula, nizitsamwitsa, ndipo sizinabala zipatso.	4:7 And some fell among thorns, and the thorns grew up, and choked it, and it yielded no fruit.
4:8 Ndipo zina zinagwa m'nthaka yabwino, ndipo zidapatsa zipatso, ndi kukula ndi kuchuluka; ndipo zinabala kupindula makumi atatu, ndi makumi asanu ndi limodzi, ndi makumi khumi.	4:8 And other fell on good ground, and did yield fruit that sprang up and increased; and brought forth, some thirty, and some sixty, and some an hundred.
4:9 Ndipo adanena kwa iwo, Amene ali nawo makutu akumva amve.	4:9 And he said unto them, He that hath ears to hear, let him hear.
4:10 Ndipo pamene adakhala pa yekha, iwo amene adali pafupi ndi Iye pamodzi ndi khumi ndi awiriwo adamfunsa Iye za mafanizo.	4:10 And when he was alone, they that were about him with the twelve asked of him the parable.
4:11 Ndipo Iye adanena nawo, Kwa inu kwapatsidwa kudziwa chinsinsi cha Ufumu wa Mulungu; koma kwa iwo ali kunja zonsezi zichitidwa m'fafanizo.	4:11 And he said unto them, Unto you it is given to know the mystery of the kingdom of God: but unto them that are without, all these things are done in parables:
4:12 Kuti kupenya apenye koma asazindikire; ndipo kumva amve, koma asadziwe; kuti pena angatembenuke mtima ndi kukhululukidwa machimo awo.	4:12 That seeing they may see, and not perceive; and hearing they may hear, and not understand; lest at any time they should be converted, and their sins should be forgiven them.
4:13 Ndipo adanena nawo, Simudziwa kodi fanizo ili? ndipo mudzazindikira bwanji mafanizo onse?	4:13 And he said unto them, Know ye not this parable? and how then will ye know all parables?
4:14 Wofesa afesa mawu.	4:14 The sower soweth the word.
4:15 Ndipo iwo ndiwo am'mbali mwa njira mofesedwamo mawu; ndipo pamene adamva, pomwepo anadza Satana nachotsa mawu wofesedwa m'mitima mwawo.	4:15 And these are they by the way side, where the word is sown; but when they have heard, Satan cometh immediately, and taketh away the word that was sown in their hearts.
4:16 Ndipo momwemonso iwo ndiwo amene afesedwa pamwala, atamva mawu, awalandira pomwepo ndi kusekerera;	4:16 And these are they likewise which are sown on stony ground; who, when they have heard the word, immediately receive it with gladness;
4:17 Ndipo alibe mizu mwa iwo wokha, koma apilira kanthawi; pamenepo pakudza masautso kapena mazunzo chifukwa cha mawu, pomwepo akhumudwa	4:17 And have no root in themselves, and so endure but for a time: afterward, when affliction or persecution ariseth for the word's sake, immediately they are offended.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
4:18 Ndipo awa ndiwo wofesedwa paminga; iwo ndiwo amene adamva mawu,	4:18 And these are they which are sown among thorns; such as hear the word,
4:19 Ndipo chisamaliro cha dziko lapansi, ndi chinyengo cha chuma, ndi kulakalaka kwa zinthu zina, zilowamo, zitsamwitsa mawu, ndipo akhala wopanda chipatso.	4:19 And the cares of this world, and the deceitfulness of riches, and the lusts of other things entering in, choke the word, and it becometh unfruitful.
4:20 Ndipo awa ndiwo wofesedwa pa nthaka yabwino ndiwo oterewa akumva mawu, nawalandira, nabala zipatso zopindula makumi atatu, ndi makumi asanu ndi limodzi, ndi makumi khumi.	4:20 And these are they which are sown on good ground; such as hear the word, and receive it, and bring forth fruit, some thirtyfold, some sixty, and some an hundred.
4:21 Ndipo adanena ndi iwo, kodi atenga nyali kuti akayibvundikire mbiya, kapena akayiyika pansu pa kama, osati kuti akayiyike pa choyikapo chake?	4:21 And he said unto them, Is a candle brought to be put under a bushel, or under a bed? and not to be set on a candlestick?
4:22 Pakuti kulibe kanthu kobisika, kamene sikadzawonetsedwa; kapena kulibe kanthu kakukhala m'seli, kamene sikadzawululidwa.	4:22 For there is nothing hid, which shall not be manifested; neither was any thing kept secret, but that it should come abroad.
4:23 Ngati munthu aliyense ali nawo makutu akumva, amve.	4:23 If any man have ears to hear, let him hear.
4:24 Ndipo adanena nawo, Samalirani chimene mukumva; ndi muyeso umene muyesa nawo udzayesedwa kwa inu; ndipo inu amene mukumva kudzawonjezedwa kwa inu.	4:24 And he said unto them, Take heed what ye hear: with what measure ye mete, it shall be measured to you: and unto you that hear shall more be given.
4:25 Pakuti kwa iye amene ali nako kanthu, kadzapatsidwa; ndipo kwa iye amene alibe kanthu, kadzachotsedwa ngakhale kanthu kali konse ali nako.	4:25 For he that hath, to him shall be given: and he that hath not, from him shall be taken even that which he hath.
4:26 Ndipo adanena, Ufumu wa Mulungu uli wotero, monga ngati munthu akataya mbewu panthaka;	4:26 And he said, So is the kingdom of God, as if a man should cast seed into the ground;
4:27 Ndipo akagona ndi kuwuka, usiku ndi usana, ndipo mbewu zikamera ndi kukula, iye sadziwa umo zichitira.	4:27 And should sleep, and rise night and day, and the seed should spring and grow up, he knoweth not how.
4:28 Pakuti nthaka ibala zipatso zake yokha; uyamba m'mera, zitsata ngala, pamenepo maso wokhwima m'ngalamo.	4:28 For the earth bringeth forth fruit of herself; first the blade, then the ear, after that the full corn in the ear.
4:29 Zikakhwima zipatso, pamenepo atumiza chikwanje, pakuti nthawi yokolola yafika.	4:29 But when the fruit is brought forth, immediately he putteth in the sickle, because the harvest is come.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
4:30 Ndipo adanena, Tidzafanizira ndi chiyani Ufumu wa Mulungu? Kapena tidzawulinganiza ndi fanizo lotani?	4:30 And he said, Whereunto shall we liken the kingdom of God? or with what comparison shall we compare it?
4:31 Uli ngati mbewu yampiru, imene ikafesedwa panthaka, ingakhale ili yaying'ono mwa mbewu zonse za padziko lapansi.	4:31 It is like a grain of mustard seed, which, when it is sown in the earth, is less than all the seeds that be in the earth:
4:32 Koma pamene ifesedwa, imela nikula koposa zitsamba zonse, nichita nthambi zazikulu; kotero kuti mbalame za mu mlengalenga zikhoza kubindikira munthunzi mwake.	4:32 But when it is sown, it groweth up, and becometh greater than all herbs, and shooteth out great branches; so that the fowls of the air may lodge under the shadow of it.
4:33 Ndipo ndi mafanizo otere ambiri adayankhula nawo mawu, monga adakhoza kumva;	4:33 And with many such parables spake he the word unto them, as they were able to hear it.
4:34 Ndipo sadayankhule nawo wopanda fanizo: koma mseli adatanthawuzira zonse kwa wophunzira ake.	4:34 But without a parable spake he not unto them: and when they were alone, he expounded all things to his disciples.
4:35 Ndipo tsiku lomwelo, pofika madzulo, adanena kwa iwo, Tiwolokere tsidya lina.	4:35 And the same day, when the even was come, he saith unto them, Let us pass over unto the other side.
4:36 Ndipo pamene adalitumiza khamulo adamtenga Iye, monga momwe adali, chombo. Ndipo padali zombo zazing'ono zina pamodzi ndi Iye.	4:36 And when they had sent away the multitude, they took him even as he was in the ship. And there were also with him other little ships.
4:37 Ndipo padawuka namondwe wamkulu wa mphepo, ndi mafunde adagabvira m'chombo, motero kuti chombo chidayamba kudzaza.	4:37 And there arose a great storm of wind, and the waves beat into the ship, so that it was now full.
4:38 Ndipo Iye mwini adali ku chiwongolero, chachombo nagona tulo, pamtsamiro; ndipo adamudzutsa Iye nanena kwa Iye, Mphunzitsi, kodi simusamala kuti tiri kuwonongeka ife?	4:38 And he was in the hinder part of the ship, asleep on a pillow: and they awake him, and say unto him, Master, carest thou not that we perish?
4:39 Ndipo adadzuka, nadzudzula mphepo, nati kwa nyanja kuti, Tonthola nukhale bata, ndipo kudagwa bata lalikulu ndipo mphepo idaleka ndikugwa bata lalikulu.	4:39 And he arose, and rebuked the wind, and said unto the sea, Peace, be still. And the wind ceased, and there was a great calm.
4:40 Ndipo adanena nawo, Muchitiranji mantha? Kufikira tsopano mulibe chikhulupiro kodi?	4:40 And he said unto them, Why are ye so fearful? how is it that ye have no faith?
4:41 Ndipo iwo adachita mantha akulu, nanena wina ndi mzake, Munthu uyu ndani nanga, kuti ingakhale mphepo ndi nyanja zimvera Iye?	4:41 And they feared exceedingly, and said one to another, What manner of man is this, that even the wind and the sea obey him?

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
<b>Mark 5</b>	<b>Mark 5</b>
5:1 Ndipo adafika tsidya lina la nyanja, ku dziko la Agerasa.	5:1 And they came over unto the other side of the sea, into the country of the Gadarenes.
5:2 Ndipo pamene adatuluka m`chombomo, pomwepo adakomana naye munthu wotuluka ku manda wogwidwa ndi mzimu wonyansa.	5:2 And when he was come out of the ship, immediately there met him out of the tombs a man with an unclean spirit,
5:3 Amene adayesa nyumba yake kumanda; ndipo panalibe munthu adakhoza kum`manganso, inde ngakhale ndi unyolo.	5:3 Who had his dwelling among the tombs; and no man could bind him, no, not with chains:
5:4 Pakuti ankamangidwa kawiri kawiri ndi matangadza ndi unyolo, ndipo adamwetula unyolo, naduladula matangadza; ndipo panalibe munthu adali ndi mphamvu yakumgwira.	5:4 Because that he had been often bound with fetters and chains, and the chains had been plucked asunder by him, and the fetters broken in pieces: neither could any man tame him.
5:5 Ndipo masiku onse, usiku ndi usana, adakhala m`mapiri ndi m`manda, nafuwula, nadzitematema ndi miyala.	5:5 And always, night and day, he was in the mountains, and in the tombs, crying, and cutting himself with stones.
5:6 Ndipo pamene adamuwona Yesu kutali, adathamanga nampembedza Iye,	5:6 But when he saw Jesus afar off, he ran and worshipped him,
5:7 Ndipo adafuwula ndi mawu akulu, nanena, Ndiri ndi chiyani ndi inu, Yesu Mwana wa Mulungu Wammwambamwamba? Ndikulumbirirani pa Mulungu musandizunze.	5:7 And cried with a loud voice, and said, What have I to do with thee, Jesus, thou Son of the most high God? I adjure thee by God, that thou torment me not.
5:8 Pakuti adanena kwa iye, Tuluka iwe, mzimu wonyansa, kwa munthuyu.	5:8 For he said unto him, Come out of the man, thou unclean spirit.
5:9 Ndipo adamfunsa iye, Dzina lako ndani? Ndipo adayankha kuti, Dzina langa ndine Legiyo; chifukwa tiri ambiri.	5:9 And he asked him, What is thy name? And he answered, saying, My name is Legion: for we are many.
5:10 Ndipo adampempha Iye kwambiri kuti asayitulutsire kunja kwake kwa dziko.	5:10 And he besought him much that he would not send them away out of the country.
5:11 Ndipo pamenepo padali gulu lalikulu la nkhumba zidali kudya kuphiri.	5:11 Now there was there nigh unto the mountains a great herd of swine feeding.
5:12 Ndipo mizimu yonse yoyipa idampempha Iye, kuti, Titumizeni ife mu nkumbazo, kuti tilowe mu izo.	5:12 And all the devils besought him, saying, Send us into the swine, that we may enter into them.
5:13 Ndipo Yesu adayilola kuti ichoke. Ndipo mizimu yonyansa idatuluka, nilowa munkhumba; ndipo gulu lidatsika ndi liwiro potsetsereka ndi kulowa m`nyanja, ndizo ngati zikwi ziwiri; ndipo zidatsamwa m`nyanja.	5:13 And forthwith Jesus gave them leave. And the unclean spirits went out, and entered into the swine: and the herd ran violently down a steep place into the sea, (they were about two thousand;) and were choked in the sea.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
5:14 Ndipo woziweta adathawa, nakanena ku m`mzinda, ndi kudziko. Ndipo adatuluka kudzawona chochitikacho.	5:14 And they that fed the swine fled, and told it in the city, and in the country. And they went out to see what it was that was done.
5:15 Ndipo anadza kwa Yesu, napenya wogwidwa ziwandayo atakhala pansu, wobvala ndi wa nzeru zake zabwino, ndiye amene adali ndi Legiyo; ndipo adawopa iwo.	5:15 And they come to Jesus, and see him that was possessed with the devil, and had the legion, sitting, and clothed, and in his right mind: and they were afraid.
5:16 Ndipo adapenyawo adawafotokozeru umo adachitira ndi wogwidwa ziwandayo, ndi za nkumbazo.	5:16 And they that saw it told them how it befell to him that was possessed with the devil, and also concerning the swine.
5:17 Ndipo adayamba kumpempha Iye kuti achoke m`malire awo.	5:17 And they began to pray him to depart out of their coasts.
5:18 Ndipo m`mene Iye adali kulowa m`chombo, adampempha waziwanda uja kuti akhale ndi Iye.	5:18 And when he was come into the ship, he that had been possessed with the devil prayed him that he might be with him.
5:19 Ndipo Yesu sadamulole, koma adanena naye, Pita kwanu kwa abwenzi ako, nuwawuze zinthu zazikulu adakuchitira Ambuye, ndi kuti adakuchitira chifundo.	5:19 Howbeit Jesus suffered him not, but saith unto him, Go home to thy friends, and tell them how great things the Lord hath done for thee, and hath had compassion on thee.
5:20 Ndipo adachoka nayamba kulalikira ku Dekapolisi zinthu zazikulu Yesu adamchitira iye; ndipo anthu onse adazizwa. Yesu achiritisa mkazi kunthenda yokha mwazi, naukitsa mwana	5:20 And he departed, and began to publish in Decapolis how great things Jesus had done for him: and all men did marvel.
5:21 Ndipo pamene Yesu adawolokanso m`chombo kupita tsidya lina, khamu lalikulu lidasokhana kwa Iye; ndipo Iye anali pambali pa nyanja.	5:21 And when Jesus was passed over again by ship unto the other side, much people gathered unto him: and he was nigh unto the sea.
5:22 Ndipo wonani, adadzako m`modzi wa akulu a sunagoge dzina lake Yairo; ndipo pakuwona, iye adagwada pamapazi ake.	5:22 And, behold, there cometh one of the rulers of the synagogue, Jairus by name; and when he saw him, he fell at his feet,
5:23 Ndipo nampepha Iye kwambiri nanena naye, kuti, Kamwana kanga kabuthu kalimkutsirizika; ndikupemphani Inu mufikeko, muyike manja anu pa iko, kuti kachiritsidwe, ndi kukhala ndi moyo.	5:23 And besought him greatly, saying, My little daughter lieth at the point of death: I pray thee, come and lay thy hands on her, that she may be healed; and she shall live.
5:24 Ndipo Yesu adamka naye pamodzi; ndipo khamu lalikulu lidamtsata Iye, ndi kumkanikiza Iye.	5:24 And Jesus went with him; and much people followed him, and thronged him.
5:25 Ndipo mkazi wina amene adali ndi nthenda ya mwazi kwa zaka khumi ndi ziwiri,	5:25 And a certain woman, which had an issue of blood twelve years,

<p><b>NYANJA</b></p>	<p><b>NEW INTERNATIONAL VERSION</b></p>
<p>5:26 Ndipo adamva zowawa zambiri mwa a sing'anga ambiri, nalipira zonse adali nazo osachira m'pang'ono ponse, koma makamaka nthenda yake idakula,</p>	<p>5:26 And had suffered many things of many physicians, and had spent all that she had, and was nothing bettered, but rather grew worse,</p>
<p>5:27 Ndipo m'mene iye adamva mbiri yake ya Yesu, anadza m'khamu kumbuyo kwake, nakhudza chobvala chake</p>	<p>5:27 When she had heard of Jesus, came in the press behind, and touched his garment.</p>
<p>5:28 Pakuti adanena iye, Ngati ndikhudza ngakhale zobvala zake ndidzachiritsidwa.</p>	<p>5:28 For she said, If I may touch but his clothes, I shall be whole.</p>
<p>5:29 Ndipo pomwepo kasupe wa nthenda yake ya mwazi idaphwa; ndipo adazindikira m'thupi kuti adachiritsidwa ku m'liri wake.</p>	<p>5:29 And straightway the fountain of her blood was dried up; and she felt in her body that she was healed of that plague.</p>
<p>5:30 Ndipo pomwepo Yesu, pamene adazindikira mwa Iye yekha kuti mphamvu idatuluka mwa Iye, adapotolokera kwa womkanikizawo, nanena, Ndani adakhudza zobvala zanga?</p>	<p>5:30 And Jesus, immediately knowing in himself that virtue had gone out of him, turned him about in the press, and said, Who touched my clothes?</p>
<p>5:31 Ndipo wophunzira ake adanena kwa Iye, Mukuwona kuti khamu liri kukanikiza Inu, ndipo munena kodi, Wandikhudza ndani?</p>	<p>5:31 And his disciples said unto him, Thou seest the multitude thronging thee, and sayest thou, Who touched me?</p>
<p>5:32 Ndipo Iye adawunguzawunguza kuti awone iye amene adachita ichi.</p>	<p>5:32 And he looked round about to see her that had done this thing.</p>
<p>5:33 Koma mkaziyo powopa ndi kunthunthumira, podziwa chimene adamchitira mwa iye, adadza, nagwa pa Iye, namuwuza Iye chowona chonse.</p>	<p>5:33 But the woman fearing and trembling, knowing what was done in her, came and fell down before him, and told him all the truth.</p>
<p>5:34 Ndipo Iye adati kwa iye, Mwana wamkaziwe, chikhulupiriro chako chakupulumutsa; pita mu mtendere, nukhale wochira kumliri wako.</p>	<p>5:34 And he said unto her, Daughter, thy faith hath made thee whole; go in peace, and be whole of thy plague.</p>
<p>5:35 M'mene Iye adali chiyankhulire, adafika a kunyumba ya mkulu wa sunagoge, nanena, kuti, Mwana wako wafa; ubvutiranjinso Mphunzitsi?</p>	<p>5:35 While he yet spake, there came from the ruler of the synagogue's house certain which said, Thy daughter is dead: why troublest thou the Master any further?</p>
<p>5:36 Mwamsanga atamva Yesu mawu adayankhulidwawo adanena kwa mkulu wa sunagoge, Usawope, khulupilira kokha.</p>	<p>5:36 As soon as Jesus heard the word that was spoken, he saith unto the ruler of the synagogue, Be not afraid, only believe.</p>
<p>5:37 Ndipo sadalole munthu aliyense kutsagana naye, koma Petro, ndi Yakobo, ndi Yohane m'bale wake wa Yakobo.</p>	<p>5:37 And he suffered no man to follow him, save Peter, and James, and John the brother of James.</p>
<p>5:38 Ndipo adafika ku nyumba kwake kwa mkulu wa sunagoge; ndipo adawona chipiringu, ndi wochita maliro ndi wokuwa ambiri.</p>	<p>5:38 And he cometh to the house of the ruler of the synagogue, and seeth the tumult, and them that wept and wailed greatly.</p>

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
5:39 Ndipo m'mene adalowa, adanena nawo, Mubuma ndi kulira chifukwa chiyani? Buthuli silidafe koma liri m'tulo.	5:39 And when he was come in, he saith unto them, Why make ye this ado, and weep? the damsel is not dead, but sleepeth.
5:40 Ndipo adamseka Iye pwepwete, koma pamene Iye adawatulutsa onse, adatenga atate ndi amake abuthulo ndi ajawo adali naye, nalowa m'mene mudali buthulo	5:40 And they laughed him to scorn. But when he had put them all out, he taketh the father and the mother of the damsel, and them that were with him, and entereth in where the damsel was lying.
5:41 Ndipo adagwira dzanja lake la buthulo, nanena kwa iye, Talita koumi; ndiko kunena posandulika, Buthu, ndinena ndi iwe. Uka.	5:41 And he took the damsel by the hand, and said unto her, Talitha cumi; which is, being interpreted, Damsel, I say unto thee, arise.
5:42 Ndipo pomwepo buthulo lidawuka niliyenda; pakuti lidali la zaka khumi ndi ziwiri. Ndipo anadabwa pomwepo ndi kudabwa kwakukulu.	5:42 And straightway the damsel arose, and walked; for she was of the age of twelve years. And they were astonished with a great astonishment.
5:43 Ndipo adawalamulira kwambiri kuti asadziwe, ichi munthu m'modzi, nawawuza kuti ampatse iye kudya.	5:43 And he charged them straitly that no man should know it; and commanded that something should be given her to eat.
<b>Mark 6</b>	<b>Mark 6</b>
6:1 Ndipo Iye adatuluka kumeneko; nafika ku dziko la kwawo; ndipo wophunzira ake adamsata.	6:1 And he went out from thence, and came into his own country; and his disciples follow him.
6:2 Ndipo pofika tsiku la sabata, adayamba kuphunzitsa m'sunagoge; ndipo ambiri adamva Iye, nazizwa, nanena, Uyu adazitenga kuti izi? Nzeru yopatsidwa kwa munthuyu njotani? Ndi zamphamvu zotere zochitidwa ndi manja ake?	6:2 And when the sabbath day was come, he began to teach in the synagogue: and many hearing him were astonished, saying, From whence hath this man these things? and what wisdom is this which is given unto him, that even such mighty works are wrought by his hands?
6:3 Kodi uyu sim'misiri wa matabwa, mwana wa Mariya, m'bale wawo wa Yakobo, ndi Yosefe, ndi Yuda, ndi Simoni? Ndipo alongo ake Sali nafe pano kodi? Ndipo adakhumudwa ndi Iye.	6:3 Is not this the carpenter, the son of Mary, the brother of James, and Joses, and of Juda, and Simon? and are not his sisters here with us? And they were offended at him.
6:4 Ndipo Yesu adanena kwa iwo, M'neneri sakhala wopanda ulemu, koma m'dziko la kwawo ndimo ndi pakati pa abale ake, ndi m'nyumba yake.	6:4 But Jesus, said unto them, A prophet is not without honour, but in his own country, and among his own kin, and in his own house.
6:5 Ndipo kumeneko sadakhoza Iye kuchita ntchito zamphamvu konse, koma kuti adayika manja ake pa anthu wodwala wowerengeka, nawachiritsa.	6:5 And he could there do no mighty work, save that he laid his hands upon a few sick folk, and healed them.
6:6 Ndipo adazizwa chifukwa cha kusakhulupirira kwawo. Ndipo adayendayenda m'midzi yozungulirapo, naphunzitsa	6:6 And he marvelled because of their unbelief. And he went round about the villages, teaching.



NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
6:7 Ndipo adadziyitanira khumi ndi awiriwo, nayamba kuwatumiza iwo awiri awiri; nawapatsa mphamvu pa mizimu yonyansa;	6:7 And he called unto him the twelve, and began to send them forth by two and two; and gave them power over unclean spirits;
6:8 Ndipo adawalamulira kuti asatenge kanthu ka pa ulendo wawo, koma ndodo yokha; asatenge lamba, mkate, kapena ndalama m'matumba awo;	6:8 And commanded them that they should take nothing for their journey, save a staff only; no scrip, no bread, no money in their purse:
6:9 Koma abvale nsapato; ndipo osati abvale malaya awiri.	6:9 But be shod with sandals; and not put on two coats.
6:10 Ndipo adanena nawo, Kumalo kuli konse mukalowa m'nyumba, khalani komweko kufikira mutachokako.	6:10 And he said unto them, In what place soever ye enter into an house, there abide till ye depart from that place.
6:11 Ndipo aliyense amene sakulandirani, kapena kumvera inu, pochoka kumeneko sansani fumbi liri ku mapazi anu, likhale mboni ya kwa iwo. Indetu ndinena ndi inu kuti patsiku la chiweruziro mlandu wa mzindawo udzakhala waukulu koposa wa Sodomu ndi Gomora.	6:11 And whosoever shall not receive you, nor hear you, when ye depart thence, shake off the dust under your feet for a testimony against them. Verily I say unto you, It shall be more tolerable for Sodom and Gomorrha in the day of judgment, than for that city.
6:12 Ndipo adatuluka nalalikira kuti anthu alape.	6:12 And they went out, and preached that men should repent.
6:13 Ndipo adatulutsa mizimu yoyipa yambiri, nadzoza mafuta anthu ambiri, wodwala, nawachiritsa.	6:13 And they cast out many devils, and anointed with oil many that were sick, and healed them.
6:14 Ndipo mfumu Herode adamva za Iye; (pakuti dzina lake lidatchuka ponse ponse) ndipo adanena, kuti, Yohane Mbatizi wauka kwa akufa, ndipo chifukwa chake ntchito za mphamvuzi zichitachita mwa Iye.	6:14 And king Herod heard of him; (for his name was spread abroad:) and he said, That John the Baptist was risen from the dead, and therefore mighty works do shew forth themselves in him.
6:15 Koma ena adanena kuti, Ndiye Eliya, Adati enanso, ndiye m'neneri, kapena m`modzi wa aneneriwo.	6:15 Others said, That it is Elias. And others said, That it is a prophet, or as one of the prophets.
6:16 Koma pamene Herode adamva, adanena, Ndi Yohane amene ndinamdula mutu, wawuka kwa akufa.	6:16 But when Herod heard thereof, he said, It is John, whom I beheaded: he is risen from the dead.
6:17 Pakuti Herode, mwini yekha, adatuma anthu namgwira Yohane, nam'manga m'nyumba ya ndende, chifukwa cha Herodiya, mkazi wa Filipino mbale wake; chifukwa adamkwatira iye.	6:17 For Herod himself had sent forth and laid hold upon John, and bound him in prison for Herodias' sake, his brother Philip's wife: for he had married her.
6:18 Pakuti Yohane adanena kwa Herode, sikuloledwa kwa inu kukhala naye mkazi wa mbale wanu.	6:18 For John had said unto Herod, It is not lawful for thee to have thy brother's wife.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
6:19 Chifukwa cha ichi adakangana momtsutsa Herodiya nafuna kumumpha iye koma adalemphera.	6:19 Therefore Herodias had a quarrel against him, and would have killed him; but she could not:
6:20 Pakuti Herode adawopa Yohane podziwa kuti adali munthu wolungama ndi woyera mtima, ndipo adamsunga iye. Ndipo pamene adamva iye, adachita zambiri, nakondwera pakumva iye.	6:20 For Herod feared John, knowing that he was a just man and an holy, and observed him; and when he heard him, he did many things, and heard him gladly.
6:21 Ndipo pamene lidafika tsiku loyenera, tsiku la kubadwa kwake kwa Herode, iye adawakonzera phwando akulu ake ndi akazembe ake ndi anthu wotchuka a ku Galileya;	6:21 And when a convenient day was come, that Herod on his birthday made a supper to his lords, high captains, and chief estates of Galilee;
6:22 Ndipo pamene mwana wa mkazi wa Herodiya adalowa yekha nabvina, adakondweretsa Herode ndi iwo wokhala naye pachakudya; ndipo mfumuyo idati kwa buthulo, Tapempha kwa ine chiri chonse uchifuna, ndidzakupatsa iwe.	6:22 And when the daughter of the said Herodias came in, and danced, and pleased Herod and them that sat with him, the king said unto the damsel, Ask of me whatsoever thou wilt, and I will give it thee.
6:23 Ndipo adamlumbirira iye, kuti, chiri chonse ukandipempha ndidzakupatsa, ngakhale kukugawira ufumu wanga.	6:23 And he sware unto her, Whatsoever thou shalt ask of me, I will give it thee, unto the half of my kingdom.
6:24 Ndipo adatuluka, nati, kwa amake, Ndizapempha chiyani? Ndipo iye adati, Mutu wake wa Yohane M'batizi.	6:24 And she went forth, and said unto her mother, What shall I ask? And she said, The head of John the Baptist.
6:25 Ndipo pomwepo adalowa mwachangu kwa mfumu, napempha kuti, Ndifuna kuti mundipatse tsopano apa, mutu wake wa Yohane M'batizi m'mbale.	6:25 And she came in straightway with haste unto the king, and asked, saying, I will that thou give me by and by in a charger the head of John the Baptist.
6:26 Ndipo mfumu idamva chisoni chachikulu; koma chifukwa cha malumbiro ake, ndi cha iwo wokhala pa chakudya, sadafune kumkaniza.	6:26 And the king was exceeding sorry; yet for his oath's sake, and for their sakes which sat with him, he would not reject her.
6:27 Ndipo pomwepo mfumu idatuma wokamumpha, namlamulira akatenge mutu wake; ndipo iye adapita namdula mutu m'nyumba ya ndende.	6:27 And immediately the king sent an executioner, and commanded his head to be brought: and he went and beheaded him in the prison,
6:28 Ndipo adamantengera mutu wake mumbale, naupereka kwa buthulo; ndipo buthulo lidaupereka kwa amake.	6:28 And brought his head in a charger, and gave it to the damsel: and the damsel gave it to her mother.
6:29 Ndipo m'mene wophunzira ake adamva, anadza nanyamula mtembo wake nawuyika m'manda.	6:29 And when his disciples heard of it, they came and took up his corpse, and laid it in a tomb.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
6:30 Ndipo atumwi adasonkhana mwa iwo wokha kwa Yesu; namuwuza zinthu ziri zonse adazichita, ndi kuziphunzitsa.	6:30 And the apostles gathered themselves together unto Jesus, and told him all things, both what they had done, and what they had taught.
6:31 Ndipo Iye adanena nawo, Idzani inu nokha padera ku malo a chipululu, mupumule kamphindi. Pakuti akudza ndi akuchoka adali piringu piringu ndipo adalibe nthawi yokwanira kuti adye	6:31 And he said unto them, Come ye yourselves apart into a desert place, and rest a while: for there were many coming and going, and they had no leisure so much as to eat.
6:32 Ndipo adachoka pa chombo kupita ku malo achipululu padera.	6:32 And they departed into a desert place by ship privately.
6:33 Ndipo anthu adawawona ali kupita, ndipo ambiri adawazindikira, nathamangira limodzi kumeneko pamtunda, nadza pamodzi kwa Iye wochokera m'mizinda yonse nawapitirira.	6:33 And the people saw them departing, and many knew him, and ran afoot thither out of all cities, and outwent them, and came together unto him.
6:34 Ndipo Yesu pamene adatuluka, nawona khamu lalikulu la anthu, anagwidwa chifundo ndi iwo, chifukwa adali ngati nkhosa zopanda mbusa; ndipo adayamba kuwaphunzitsa zinthu zambiri.	6:34 And Jesus, when he came out, saw much people, and was moved with compassion toward them, because they were as sheep not having a shepherd: and he began to teach them many things.
6:35 Ndipo pamene tsiku lidapendeka ndithu, anadza kwa Iye wophunzira ake, nanena, Malo ano nga chipululu, ndipo nthawi yatha ndithu.	6:35 And when the day was now far spent, his disciples came unto him, and said, This is a desert place, and now the time is far passed:
6:36 Muwatumize iwo kuti apite, alowe ku milaga ndi ku midzi yozungulira, kuti akadzigulire wokha kanthu kakudya. Pakuti alibe kanthu kakudya.	6:36 Send them away, that they may go into the country round about, and into the villages, and buy themselves bread: for they have nothing to eat.
6:37 Koma Iye adayankha nati kwa iwo, Apatseni kudya ndinu. Ndipo iwo adanena naye, kodi tipite ife ndi kugula mikate ya makobiri mazana awiri ndi kuwapatsa kudya?	6:37 He answered and said unto them, Give ye them to eat. And they say unto him, Shall we go and buy two hundred pennyworth of bread, and give them to eat?
6:38 Ndipo Iye adanena kwa iwo, kuti, Muli nayo mikate ingati? Pitani mukawone. Ndipo m'mene adadziwa adanena, Isanu ndi nsomba ziwiri.	6:38 He saith unto them, How many loaves have ye? go and see. And when they knew, they say, Five, and two fishes.
6:39 Ndipo adawalamulira kuti akhalitse pansoni onse magulu magulu pawudzu.	6:39 And he commanded them to make all sit down by companies upon the green grass.
6:40 Ndipo adakhala pansi mabungwe mabungwe a makumi khumi ndi a makumi asanu.	6:40 And they sat down in ranks, by hundreds, and by fifties.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
6:41 Ndipo pamene Iye adatenga mikate isanuyo ndi nsomba ziwirizo adayang'ana kumwamba, nadalitsa, nagawa mikate; napatsa iyo kwa wophunzira kuti apereke kwa iwo; ndi nsomba ziwiri adagawira onsewo.	6:41 And when he had taken the five loaves and the two fishes, he looked up to heaven, and blessed, and brake the loaves, and gave them to his disciples to set before them; and the two fishes divided he among them all.
6:42 Ndipo anadya iwo onse, nakhuta.	6:42 And they did all eat, and were filled.
6:43 Ndipo adatola makombo, mitanga khumi ndi iwiri, ndiponso za nsomba.	6:43 And they took up twelve baskets full of the fragments, and of the fishes.
6:44 Ndipo amene adadya mikateyo adali amuna zikwi zisanu.	6:44 And they that did eat of the loaves were about five thousand men.
6:45 Ndipo pomwepo Iye adalamulira wophunzira ake alowe m`chombo, ndi kutsogolera kupita kutsidya lija ku Betsayida, m'mene Iye yekha adali kuwuzwa khamulo kuti lichoke.	6:45 And straightway he constrained his disciples to get into the ship, and to go to the other side before unto Bethsaida, while he sent away the people.
6:46 Ndipo atatsanzikana nalo, adachoka Iye, nalowa m'phiri kukapemphera.	6:46 And when he had sent them away, he departed into a mountain to pray.
6:47 Ndipo pofika madzulo chombo chidali pakati pa nyanja, ndi Iye yekha adali pamtunda.	6:47 And when even was come, the ship was in the midst of the sea, and he alone on the land.
6:48 Ndipo pakuwawona ali kubvutika ndi kupalasa, pakuti mphepo idadza mokomana nawo, ndipo pa ulonda wachinayi wa usiku Iye anadza kwa iwo, alikuyenda pamwamba pa nyanja; nati awapitirire.	6:48 And he saw them toiling in rowing; for the wind was contrary unto them: and about the fourth watch of the night he cometh unto them, walking upon the sea, and would have passed by them.
6:49 Koma iwo, pamene adamuwona Iye alikuyenda panyanja, adayesa kuti ndi mzungu, nafuwula:	6:49 But when they saw him walking upon the sea, they supposed it had been a spirit, and cried out:
6:50 Pakuti iwo onse adamuwona Iye, nabvutika. Koma pomwepo adawayankhula nanena kwa iwo, Kondwerani; Ndinetu, musawope.	6:50 For they all saw him, and were troubled. And immediately he talked with them, and saith unto them, Be of good cheer: it is I; be not afraid.
6:51 Ndipo Iye adakwera, nalowa kwa iwo chombo, ndipo mphepo idaleka; ndipo anadabwa kwakukulu koposa muyeso mwa iwo wokha.	6:51 And he went up unto them into the ship; and the wind ceased: and they were sore amazed in themselves beyond measure, and wondered.
6:52 Pakuti sadazindikire za chozizwitsa cha mikateyo, pakuti mitima yawo idawumitsidwa.	6:52 For they considered not the miracle of the loaves: for their heart was hardened.
6:53 Ndipo atawoloka iwo, adafika pamtunda ku Genesarete, nakocheza padowoko.	6:53 And when they had passed over, they came into the land of Gennesaret, and drew to the shore.
6:54 Ndipo pamene adatuluka m'chombo adamzindikira Iye pomwepo.	6:54 And when they were come out of the ship, straightway they knew him,

<p><b>NYANJA</b></p>	<p><b>NEW INTERNATIONAL VERSION</b></p>
<p>6:55 Ndipo adathamanga dziko lonselo mozungulira nayamba kunyamula anthu wodwala pamphasa zawo, kufika nawo kumene adamva kuti analiko Iye.</p>	<p>6:55 And ran through that whole region round about, and began to carry about in beds those that were sick, where they heard he was.</p>
<p>6:56 Ndipo kumene kulikonse adalowa Iye m'midzi, kapena m'mizinda, kapena m'milaga, anthu adagoneka wodwala m`misewu, nampempha Iye kuti akakhudze ngakhale mphonje yokha ya chobvala chake; ndipo onse amene adamkhudza adachiritsidwa.</p>	<p>6:56 And whithersoever he entered, into villages, or cities, or country, they laid the sick in the streets, and besought him that they might touch if it were but the border of his garment: and as many as touched him were made whole.</p>
<p><b>Mark 7</b></p>	<p><b>Mark 7</b></p>
<p>7:1 Ndipo adasonkhana kwa Iye Afarisi, ndi ena alembi, wochokera ku Yerusalemu.</p>	<p>7:1 Then came together unto him the Pharisees, and certain of the scribes, which came from Jerusalem.</p>
<p>7:2 Ndipo pamene adawona ena a wophunzira ake akudya mkate ndi m'manja mwakuda, ndi mosasamba, adampezerapo chifukwa.</p>	<p>7:2 And when they saw some of his disciples eat bread with defiled, that is to say, with unwashen, hands, they found fault.</p>
<p>7:3 Pakuti Afarisi, ndi Ayuda onse samadya osasamba m'manja mwawo, kuti asunge mwambo wa akulu.</p>	<p>7:3 For the Pharisees, and all the Jews, except they wash their hands oft, eat not, holding the tradition of the elders.</p>
<p>7:4 Ndipo pochokera ku m'sika, sakudya asanasambe m'thupi; ndipo zilipo zinthu zina zambiri adazilandira kuzisunga, ndizo matsukidwe a zikho, ndi miphika, ndi zotengera zamkuwa ndi magome.</p>	<p>7:4 And when they come from the market, except they wash, they eat not. And many other things there be, which they have received to hold, as the washing of cups, and pots, brasen vessels, and of tables.</p>
<p>7:5 Ndipo Afarisi ndi alembi adamfunsa Iye, Bwanji wophunzira anu satsata mwambo wa akulu, koma akudya mkate wawo ndi m'manja mwakuda?</p>	<p>7:5 Then the Pharisees and scribes asked him, Why walk not thy disciples according to the tradition of the elders, but eat bread with unwashen hands?</p>
<p>7:6 Iye adawayankha nati kwa iwo, Yesaya adanenera bwino za inu wonyenga, monga kwalembedwa, Anthu awa andilemekeza Ine ndi milomo yawo, koma mitima yawo ikhala kutali ndi Ine.</p>	<p>7:6 He answered and said unto them, Well hath Esaias prophesied of you hypocrites, as it is written, This people honoureth me with their lips, but their heart is far from me.</p>
<p>7:7 Koma andilambira Ine kwa chabe, ndi kuphunzitsa ziphunzitso za malamulo a anthu.</p>	<p>7:7 Howbeit in vain do they worship me, teaching for doctrines the commandments of men.</p>
<p>7:8 Musiya lamulo la Mulungu, nimusunga mwambo wa anthu, monga kutsuka miphika ndi zikho; ndi zinthu zina zambiri zimene muchita.</p>	<p>7:8 For laying aside the commandment of God, ye hold the tradition of men, as the washing of pots and cups: and many other such like things ye do.</p>
<p>7:9 Ndipo adanena nawo, Mochenjera mukaniza lamulo la Mulungu, kuti musunge mwambo wanu.</p>	<p>7:9 And he said unto them, Full well ye reject the commandment of God, that ye may keep your own tradition.</p>

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
7:10 Pakuti Mose adati, Lemekeza atate wako ndi amako; ndipo iye wonenera zoyipa atate wake kapena amayi wake, afe imfa:	7:10 For Moses said, Honour thy father and thy mother; and, Whoso curseth father or mother, let him die the death:
7:11 Koma inu munena, Ngati munthu akati kwa atate wake, kapena amayi wake, Korbani, ndiko kuti mphatso imene ukadathandizidwa nayo ndi ine; adzakhala womasulidwa.	7:11 But ye say, If a man shall say to his father or mother, It is Corban, that is to say, a gift, by whatsoever thou mightest be profited by me; he shall be free.
7:12 Ndipo simulolanso kumchitira kanthu atate wake kapena amayi wake;	7:12 And ye suffer him no more to do ought for his father or his mother;
7:13 Muyesa achabe mawu a Mulungu monga mwa mwambo wanu, umene mudaupereka; ndi zinthu zotere zambiri muzichita.	7:13 Making the word of God of none effect through your tradition, which ye have delivered: and many such like things do ye.
7:14 Ndipo pamene adadziyitaniranso khamu la anthu kwa Iye, adanena nawo, Mverani Ine nonsenu ndipo mudziwitse:	7:14 And when he had called all the people unto him, he said unto them, Hearken unto me every one of you, and understand:
7:15 Kulibe kanthu kunja kwa munthu kolowa mwa iye, kangathe kumdetsa: koma zinthu zotuluka mwa iye, ndizo zomdetsa munthu.	7:15 There is nothing from without a man, that entering into him can defile him: but the things which come out of him, those are they that defile the man.
7:16 Ngati munthu ali nawo makutu akumva, muloleni amve.	7:16 If any man have ears to hear, let him hear.
7:17 Ndipo m'mene Iye adalowa m'nyumba kusiyana ndi khamulo, wophunzira ake adamfunsa Iye za fanizolo.	7:17 And when he was entered into the house from the people, his disciples asked him concerning the parable.
7:18 Ndipo adanena nawo, Inunso mukhala wopanda nzeru kodi? Kodi simuzindikira kuti kanthu kali konse kochokera kunja kolowa mwa munthu sikangathe kumdetsa iye;	7:18 And he saith unto them, Are ye so without understanding also? Do ye not perceive, that whatsoever thing from without entereth into the man, it cannot defile him;
7:19 Chifukwa sikalowa mumtima mwake, koma m'mimba mwake, ndipo katulukira kuthengo ndipo potero adayeretsa zakudya zonse.	7:19 Because it entereth not into his heart, but into the belly, and goeth out into the draught, purging all meats?
7:20 Ndipo adati, chotuluka mwa munthu ndicho chidetsa munthu.	7:20 And he said, That which cometh out of the man, that defileth the man.
7:21 Pakuti m'kati mwake mwa mitima ya anthu mutuluka maganizo woyipa, za chigololo, chiwerewere, kupha,	7:21 For from within, out of the heart of men, proceed evil thoughts, adulteries, fornications, murders,
7:22 Kuba, kusilira kuchita zoyipa, chinyengo, chinyanso, diso loyipa, mwano, kudzikuzi, kupusa:	7:22 Thefts, covetousness, wickedness, deceit, lasciviousness, an evil eye, blasphemy, pride, foolishness:
7:23 Zoyipa izi zonse zichokera mkati nizidetsa munthu.	7:23 All these evil things come from within, and defile the man.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
7:24 Ndipo Iye adawuka nachoka kumeneko, nanka ku malire a ku Turo ndi Sidoni. Ndipo adalowa m’nyumba, nafuna kuti asadziwe munthu aliyense; ndipo sadakhoza kubisika.	7:24 And from thence he arose, and went into the borders of Tyre and Sidon, and entered into an house, and would have no man know it: but he could not be hid.
7:25 Pakuti mkazi wina amene adali ndi kabuthu kake kamene kadali ndi mzimu wonyansa. Pamene adamva za Iye, anadza, nagwa pa mapazi ake.	7:25 For a certain woman, whose young daughter had an unclean spirit, heard of him, and came and fell at his feet:
7:26 Koma mkaziyo adali Mhelene, mtundu wake Msuro-Fonika. Ndipo adampempha Iye kuti atulutse chiwanda mwa mwana wake.	7:26 The woman was a Greek, a Syrophenician by nation; and she besought him that he would cast forth the devil out of her daughter.
7:27 Koma Yesu adanena naye, Baleka, ayambe akhuta ana; pakuti sibwino kutenga mkate wa ana, ndi kuwutayira tiagalu.	7:27 But Jesus said unto her, Let the children first be filled: for it is not meet to take the children's bread, and to cast it unto the dogs.
7:28 Ndipo iye adayankha nati kwa Iye, Inde Ambuye: tingakhale tiagalu tapansi pa gome timadyako nyenyiswa za ana.	7:28 And she answered and said unto him, Yes, Lord: yet the dogs under the table eat of the children's crumbs.
7:29 Ndipo adati kwa iye, Chifukwa cha mawu amenewa, Pita; chiwanda chatuluka mwa mwana wako wamkazi.	7:29 And he said unto her, For this saying go thy way; the devil is gone out of thy daughter.
7:30 Ndipo pamene adafika kunyumba kwake, adapeza mwana wakeyo atamgoneka pakama, ndi chiwanda chitatuluka.	7:30 And when she was come to her house, she found the devil gone out, and her daughter laid upon the bed.
7:31 Ndipo adatulukanso m’malire a ku Turo, ndi Sidoni, adafika ku nyanja ya Galileya, kupyola pakati pa mayiko a Dekapoli.	7:31 And again, departing from the coasts of Tyre and Sidon, he came unto the sea of Galilee, through the midst of the coasts of Decapolis.
7:32 Ndipo anadza naye kwa Iye munthu wogontha, ndi wa chibwibwi; ndipo adampempha Iye kuti ayike manja ake pa iye.	7:32 And they bring unto him one that was deaf, and had an impediment in his speech; and they beseech him to put his hand upon him.
7:33 Ndipo adampatula pa khamu la anthu pa yekha, namulonga zala zake m’makutu mwake, nalabvula malobvu, nakhudza lilime lake;	7:33 And he took him aside from the multitude, and put his fingers into his ears, and he spit, and touched his tongue;
7:34 Ndipo pakuyang`ana kumwamba, adawusa moyo, nanena kwa iye Efata ndiko kuti, Tatseguka.	7:34 And looking up to heaven, he sighed, and saith unto him, Ephphatha, that is, Be opened.
7:35 Ndipo pomwepo makutu ake adatseguka, ndipo chomangira lilime lake chidamasulidwa ndipo adayankhula chilunjikire.	7:35 And straightway his ears were opened, and the string of his tongue was loosed, and he spake plain.
7:36 Ndipo adalengeza kopambana kuti asawuze munthu aliyense; koma monga momwe Iye adawalamulitsa momwense makamaka adalengeza kopambana.	7:36 And he charged them that they should tell no man: but the more he charged them, so much the more a great deal they published it;

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
7:37 Ndipo anadabwa kwakukulu, koposa muyeso nanena, Wachita Iye zonse bwino; angakhale wogontha awamvetsa, ndi wosayankhula awayankhulitsa.	7:37 And were beyond measure astonished, saying, He hath done all things well: he maketh both the deaf to hear, and the dumb to speak.
<b>Mark 8</b>	<b>Mark 8</b>
8:1 Masiku amenewo pakukhalanso khamu lalikulu la anthu, ndipo analibe kanthu kakudya, Yesu adadziyitanira wophunzira ake kwa Iye yekha, nanena nawo.	8:1 In those days the multitude being very great, and having nothing to eat, Jesus called his disciples unto him, and saith unto them,
8:2 Ndikumva nalo chifundo khamulo, chifukwa ali ndi Ine chikhalire masiku atatu, ndipo alibe kanthu kakudya.	8:2 I have compassion on the multitude, because they have now been with me three days, and have nothing to eat:
8:3 Ndipo ngati ndiwawuza iwo kuti azipita kwawo osadya kanthu, adzakomoka panjira; ndipo ena a iwo achokera kutali.	8:3 And if I send them away fasting to their own houses, they will faint by the way: for divers of them came from far.
8:4 Ndipo wophunzira ake adamuyankha Iye, Munthu adzatha kutenga kuti mikate yokhutitsa anthu awa m'chipululu muno?	8:4 And his disciples answered him, From whence can a man satisfy these men with bread here in the wilderness?
8:5 Ndipo adawafunsa iwo, Muli nayo mikate ingati? Ndipo adati, Isanu ndi iwiri.	8:5 And he asked them, How many loaves have ye? And they said, Seven.
8:6 Ndipo adalamulira anthu kuti akhale pans; natenga mikate isanu ndi iwiriyo, nayamika, nanyema, napatsa wophunzira ake, kuti apereke kwa iwo; ndipo adapereka kwa anthuwo.	8:6 And he commanded the people to sit down on the ground: and he took the seven loaves, and gave thanks, and brake, and gave to his disciples to set before them; and they did set them before the people.
8:7 Ndipo adali nato tinsomba towerengeka; ndipo Iye anadalitsa, nalamulira kuti iwo atipereke itonso.	8:7 And they had a few small fishes: and he blessed, and commanded to set them also before them.
8:8 Ndipo adadya, nakhuta; ndipo adatola makombo madengu asanu ndi awiri.	8:8 So they did eat, and were filled: and they took up of the broken meat that was left seven baskets.
8:9 Ndipo iwo amene adadya adali ngati zikwi zinayi; ndipo Iye adawatumiza apite.	8:9 And they that had eaten were about four thousand: and he sent them away.
8:10 Ndipo pomwepo adalowa m'chombo ndi wophunzira ake, ndipo adafika ku mbali ya ku Dalimanuta.	8:10 And straightway he entered into a ship with his disciples, and came into the parts of Dalmanutha.
8:11 Ndipo Afarisi adatuluka, nayamba kufunsana naye, ndi kufuna kwa Iye chizindikiro chochokera kumwamba, kumuyesa Iye.	8:11 And the Pharisees came forth, and began to question with him, seeking of him a sign from heaven, tempting him.



NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
8:12 Ndipo adawusa moyo mu mzimu wake, nanena, Anthu a m’badwo uno afunafuna chizindikiro bwanji? Indetu ndinena kwa inu, ngati Chizindikiro sichidzapatsidwa kwa m’badwo uno!	8:12 And he sighed deeply in his spirit, and saith, Why doth this generation seek after a sign? verily I say unto you, There shall no sign be given unto this generation.
8:13 Ndipo adawasiya iwo, nalowanso m’chombo, nachoka kupita kutsidya lina.	8:13 And he left them, and entering into the ship again departed to the other side.
8:14 Ndipo wophunzira adayiwalala kutenga mikate, ndipo adalibe mkate m’chombo koma umodzi wokha.	8:14 Now the disciples had forgotten to take bread, neither had they in the ship with them more than one loaf.
8:15 Ndipo Iye adawalamulira iwo, nanena, chenjerani, penyani kuti mupewe chotupitsa mkate cha Afarisi, ndi chotupitsa mkate cha Herode.	8:15 And he charged them, saying, Take heed, beware of the leaven of the Pharisees, and of the leaven of Herod.
8:16 Ndipo adatsutsana wina ndi mzake, nanena kuti, chifukwa chakuti tiribe mikate.	8:16 And they reasoned among themselves, saying, It is because we have no bread.
8:17 Ndipo pamene Yesu adazindikira, adanena nawo, Bwanji mukutsutsana chifukwa mulibe mkate? Kodi kufikira tsopano simuzindikira, ndikudziwitsa? Kodi mitima yanu ndi yowuma?	8:17 And when Jesus knew it, he saith unto them, Why reason ye, because ye have no bread? perceive ye not yet, neither understand? have ye your heart yet hardened?
8:18 Pokhala nawo maso simupenya kodi? Ndipokhala nawo makutu simukumva kodi? Ndipo simukumbukira kodi?	8:18 Having eyes, see ye not? and having ears, hear ye not? and do ye not remember?
8:19 Pamene tidanyema mikate isanu ndi kugawira kwa anthu zikwi zisanu, Kodi mudatola mitanga ingati yodzala ndi makombo? Iwo adanena kwa Iye, khumi ndi iwiri.	8:19 When I brake the five loaves among five thousand, how many baskets full of fragments took ye up? They say unto him, Twelve.
8:20 Ndipo mikate isanu ndi iwiri kwa anthu zikwi zinayi, mudatola mitanga ingati yodzala ndi makombo? Ndipo adanena, Isanu ndi iwiri.	8:20 And when the seven among four thousand, how many baskets full of fragments took ye up? And they said, Seven.
8:21 Ndipo Iye adanena nawo, Nanga n’chifukwa chiyani simukuzindikira?	8:21 And he said unto them, How is it that ye do not understand?
8:22 Ndipo anadza ku Betsaida; ndipo anadza naye kwa Iye munthu wakhungu, nampempha Iye kuti amkhudze iye.	8:22 And he cometh to Betsaida; and they bring a blind man unto him, and besought him to touch him.
8:23 Ndipo adamgwira dzanja munthu wakhunguyo, natulukira naye kunja kwa mzinda; ndipo atamthira malobvu m’maso mwake, nayika manja pa iye, adamfunsa iye, Uwona kanthu kodi?	8:23 And he took the blind man by the hand, and led him out of the town; and when he had spit on his eyes, and put his hands upon him, he asked him if he saw ought.
8:24 Ndipo adakweza maso, nanena ndikuwona anthu; pakuti ndiwapenya ayendayenda ngati mitengo.	8:24 And he looked up, and said, I see men as trees, walking.

<p><b>NYANJA</b></p>	<p><b>NEW INTERNATIONAL VERSION</b></p>
<p>8:25 Patatha izi adayikanso manja m’maso mwake, ndipo adampenyetsa kumwamba, nachiritsidwa, nawona munthu aliyense bwino bwino.</p>	<p>8:25 After that he put his hands again upon his eyes, and made him look up: and he was restored, and saw every man clearly.</p>
<p>8:26 Ndipo adamtumiza apite kwawo, nanena, Usalowe konse m’muzinda kapena kuwuzwa wina ali yense mumzinda</p>	<p>8:26 And he sent him away to his house, saying, Neither go into the town, nor tell it to any in the town.</p>
<p>8:27 Ndipo adatuluka Yesu ndi wophunzira ake, nalowa ku mizinda ya ku Kayisareya wa Filipi; ndipo panjira adawafunsa wophunzira ake, nanena nawo, Kodi anthu amanena kuti Ine ndine yani?</p>	<p>8:27 And Jesus went out, and his disciples, into the towns of Caesarea Philippi: and by the way he asked his disciples, saying unto them, Whom do men say that I am?</p>
<p>8:28 Ndipo adayankha nati, Yohane M’batizi; ndi ena Eliya; koma ena, M’modzi wa aneneri.</p>	<p>8:28 And they answered, John the Baptist; but some say, Elias; and others, One of the prophets.</p>
<p>8:29 Ndipo Iye adati kwa iwo, Koma inu munena kuti ndine yani? Petro adayankha nanena naye, Ndinu Khristu.</p>	<p>8:29 And he saith unto them, But whom say ye that I am? And Peter answereth and saith unto him, Thou art the Christ.</p>
<p>8:30 Ndipo adawalamulira iwo kuti asawuze munthu ndi m’modzi za Iye.</p>	<p>8:30 And he charged them that they should tell no man of him.</p>
<p>8:31 Ndipo adayamba kuwaphunzitsa, kuti kuyenera kuti Mwana wa munthu akamve zowawa zambiri, nakakanidwe ndi akulu ndi ansembe akulu, ndi alembi, nakaphedwe, ndipo pakutha masiku atatu akawuke.</p>	<p>8:31 And he began to teach them, that the Son of man must suffer many things, and be rejected of the elders, and of the chief priests, and scribes, and be killed, and after three days rise again.</p>
<p>8:32 Ndipo mawuwo adanena poyera. Ndipo Petro adamtenga Iye, nayamba kumdzudzula Iye.</p>	<p>8:32 And he spake that saying openly. And Peter took him, and began to rebuke him.</p>
<p>8:33 Koma pamene adapotoloka, napenya wophunzira ake, adamdzudzula Petro, nanena, Choka, pita kumbuyo kwanga, Satana iwe; popeza susamalira zinthu za Mulungu koma za anthu.</p>	<p>8:33 But when he had turned about and looked on his disciples, he rebuked Peter, saying, Get thee behind me, Satan: for thou savourest not the things that be of God, but the things that be of men.</p>
<p>8:34 Ndipo pamene adadziyitanira anthu pamodzi ndi wophunzira ake, adati kwa iwo, Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikanize yekha, nanyamule mtanda wake, nanditsate Ine.</p>	<p>8:34 And when he had called the people unto him with his disciples also, he said unto them, Whosoever will come after me, let him deny himself, and take up his cross, and follow me.</p>
<p>8:35 Pakuti aliyense wofuna kupulumutsa moyo wake adzawutaya; ndipo yense wotaya moyo wake chifukwa cha Ine, ndi chifukwa cha Uthenga Wabwino adzaupulumutsa.</p>	<p>8:35 For whosoever will save his life shall lose it; but whosoever shall lose his life for my sake and the gospel's, the same shall save it.</p>

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
8:36 Pakuti munthu apindulanji akadzilemeleretsa dziko lonse lapansi, natayapo moyo wake?	8:36 For what shall it profit a man, if he shall gain the whole world, and lose his own soul?
8:37 Kapena munthu adzapereka chiyani chosinthana ndi moyo wake?	8:37 Or what shall a man give in exchange for his soul?
8:38 Pakuti aliyense wochita manyazi chifukwa cha Ine, ndi cha mawu anga mu m'badwo uno wachigololo ndi wochimwa. Mwana wa munthu adzachitanso manyazi chifukwa cha iyeyu, pamene Iye adzafika nawo angelo ake woyera, mu ulemerero wa Atate wake.	8:38 Whosoever therefore shall be ashamed of me and of my words in this adulterous and sinful generation; of him also shall the Son of man be ashamed, when he cometh in the glory of his Father with the holy angels.
<b>Mark 9</b>	<b>Mark 9</b>
9:1 Ndipo adanena nawo, Indetu ndinena ndi inu kuti, Alipo ena ayimilira pano, amene sadzalawa imfa konse, kufikira atawona Ufumu wa Mulungu utadza ndi mphamvu.	9:1 And he said unto them, Verily I say unto you, That there be some of them that stand here, which shall not taste of death, till they have seen the kingdom of God come with power.
9:2 Ndipo atapita masiku asanu ndi limodzi, Yesu adatenga Petro, ndi Yakobo ndi Yohane, nakwera nawo pa phiri lalitali padera pa wokha; ndipo adasinthika pamaso pawo:	9:2 And after six days Jesus taketh with him Peter, and James, and John, and leadeth them up into an high mountain apart by themselves: and he was transfigured before them.
9:3 Ndipo zobvala zake zidakhala zonyezimira, zoyera mbu kuposa; monga ngati muwomba wotsuka nsalu pa dziko lapansi sangathe kuziyeretsayi.	9:3 And his raiment became shining, exceeding white as snow; so as no fuller on earth can white them.
9:4 Ndipo adawonekera kwa iwo Eliya ndi Mose, alikuyankhulana ndi Yesu.	9:4 And there appeared unto them Elias with Moses: and they were talking with Jesus.
9:5 Ndipo Petro adayankha, nanena ndi Yesu, Rabi, Kutikomera ife kukhala pano; ndipo timange mahema atatu; imodzi yanu, ndi wina wa Mose ndi wina wa Eliya.	9:5 And Peter answered and said to Jesus, Master, it is good for us to be here: and let us make three tabernacles; one for thee, and one for Moses, and one for Elias.
9:6 Pakuti sadadziwa chimene adzanena; chifukwa adachita mantha ndithu.	9:6 For he wist not what to say; for they were sore afraid.
9:7 Ndipo padadza mtambo wophimba iwo, ndipo mawu adatuluka mu mtambowo, kuti, Uyu ndiye Mwana wanga wokondedwa; mverani Iye.	9:7 And there was a cloud that overshadowed them: and a voice came out of the cloud, saying, This is my beloved Son: hear him.
9:8 Ndipo dzidzidzi powunguzawunguza, sadapenya munthu wina yense, koma Yesu yekha, ndi iwo eni.	9:8 And suddenly, when they had looked round about, they saw no man any more, save Jesus only with themselves.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
9:9 Ndipo pakutsika iwo paphiri, Iye adawalamulira kuti asawuze munthu aliyense zinthu zimene adaziwona kufikira pamene Mwana wa munthu akadzawuka kwa akufa ndipo.	9:9 And as they came down from the mountain, he charged them that they should tell no man what things they had seen, till the Son of man were risen from the dead.
9:10 Ndipo adasunga mawuwo mwa iwo wokha, nafunsana mwa iwo wokha, kuti kuwuka kwa akufa kutanthawuzanji?	9:10 And they kept that saying with themselves, questioning one with another what the rising from the dead should mean.
9:11 Ndipo adamfunsa Iye, nanena, Nanga alembi anena bwanji kuti adzayamba kufika Eliya?	9:11 And they asked him, saying, Why say the scribes that Elias must first come?
9:12 Ndipo Iye adayankha nanena nawo, Eliya ayamba kudza ndithu, nadzabwezeretsa zinthu zonse; nanga zalembedwa bwanji za Mwana wa munthu, kuti ayenera kumva zowawa zambiri ndi kuyesedwa chabe?	9:12 And he answered and told them, Elias verily cometh first, and restoreth all things; and how it is written of the Son of man, that he must suffer many things, and be set at nought.
9:13 Koma ndinena ndi inu Kuti Eliya adabwera kale, ndipo adamchitiranso ziri zonse iwo adazifuna, monga kwalembedwa za iye.	9:13 But I say unto you, That Elias is indeed come, and they have done unto him whatsoever they listed, as it is written of him.
9:14 Ndipo pamene anadza kwa wophunzira ake, adawona khamu lalikulu la anthu wozungulira iwo, ndi alembi alikufunsana nawo.	9:14 And when he came to his disciples, he saw a great multitude about them, and the scribes questioning with them.
9:15 Ndipo pomwepo anthu onse, pakumuwona Iye, adazizwa kwambiri, namthamangira Iye, namulonjera.	9:15 And straightway all the people, when they beheld him, were greatly amazed, and running to him saluted him.
9:16 Ndipo adafunsa alembi, Mufunsana nawo chiyani?	9:16 And he asked the scribes, What question ye with them?
9:17 Ndipo wina wa m'khamulo adamyankha Iye, kuti, Mphunzitsi, ndadza naye kwa Inu mwana wanga, ali nawo mzimu wosayankhula;	9:17 And one of the multitude answered and said, Master, I have brought unto thee my son, which hath a dumb spirit;
9:18 Ndipoponse pamene umtenga iye, ung`amba iye; ndipo achita thobvu, nakukuta mano, nanyololoka; ndipo ndidayankhula nawo wophunzira anu kuti awutulutse; koma sadakhoza.	9:18 And wheresoever he taketh him, he teareth him: and he foameth, and gnasheth with his teeth, and pineth away: and I spake to thy disciples that they should cast him out; and they could not.
9:19 Ndipo Iye adawayankha iwo nanena, M'bado wosakhulupirira inu, ndidzakhala ndi inu nthawi yaitali yanji? Ndidzakulekererani nthawi yanji? Mudze naye kwa Ine.	9:19 He answereth him, and saith, O faithless generation, how long shall I be with you? how long shall I suffer you? bring him unto me.
9:20 Ndipo anadza naye kwa Iye; ndipo pakumuwona iye, pomwepo mzimuwo udam`ng`amba kowopsa; ndipo adagwa pansi nabvimbinika ndi kuchita thobvu.	9:20 And they brought him unto him: and when he saw him, straightway the spirit tare him; and he fell on the ground, and wallowed foaming.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
9:21 Ndipo Iye adafunsa atate wake, kuti chimenechi chidayamba liti kumgwira? Ndipo adati, akali mwana.	9:21 And he asked his father, How long is it ago since this came unto him? And he said, Of a child.
9:22 Ndipo kawiri kawiri umamtaya kumoto ndi kumadzi, kumuwononga iye; koma ngati mukhoza kuchita kanthu tithandizeni, ndi kutichitira chifundo.	9:22 And ofttimes it hath cast him into the fire, and into the waters, to destroy him: but if thou canst do any thing, have compassion on us, and help us.
9:23 Ndipo Yesu adanena naye, Ngati mukhulupilirira, zinthu zonse zitheka kwa iye wokhulupirira.	9:23 Jesus said unto him, If thou canst believe, all things are possible to him that believeth.
9:24 Pomwepo atate wa mwana adafuwula, nanena ndi misozi, Ambuye, Ndikhulupirira; thandizani kusakhulupirira kwanga.	9:24 And straightway the father of the child cried out, and said with tears, Lord, I believe; help thou mine unbelief.
9:25 Ndipo pamene Yesu adawona kuti khamu la anthu liri kuthamangira pamodzi, adadzudzula mzimu woyipawo, nanena ndi uwo, mzimu wosayankhula ndi wongontha iwe, tuluka mwa iye, ndipo usalowenso mwa iye.	9:25 When Jesus saw that the people came running together, he rebuked the foul spirit, saying unto him, Thou dumb and deaf spirit, I charge thee, come out of him, and enter no more into him.
9:26 Ndipo mzimu udafuwula, num'ngambitsa, udatuluka, ndipo mwana adakhala ngati wakufa, kotero kuti ambiri ananena, Wamwalira.	9:26 And the spirit cried, and rent him sore, and came out of him: and he was as one dead; insomuch that many said, He is dead.
9:27 Koma Yesu adagwira dzanja lake, nam'nyamutsa; ndipo adayimilira.	9:27 But Jesus took him by the hand, and lifted him up; and he arose.
9:28 Ndipo pamene Iye adalowa m'nyumba, wophunzira ake adafunsa mtseri kuti, Nanga bwanji sitinakhoza ife kuwutulutsa?	9:28 And when he was come into the house, his disciples asked him privately, Why could not we cast him out?
9:29 Ndipo Iye adati kwa iwo, Mtundu uwu sukhoza kutuluka ndi kanthu kena konse, koma ndi pemphero ndi kusala kudya.	9:29 And he said unto them, This kind can come forth by nothing, but by prayer and fasting.
9:30 Ndipo adachoka iwo kumeneko, napyola pakati pa Galileya; ndipo Iye sadafune kuti munthu aliyense adziwe.	9:30 And they departed thence, and passed through Galilee; and he would not that any man should know it.
9:31 Pakuti adaphunzitsa wophunzira ake, nanena nawo kuti, Mwana wa munthu aperekedwa m'manja mwa anthu, ndipo adzamupha Iye; ndipo ataphedwa, adzawukanso tsiku lachitatu.	9:31 For he taught his disciples, and said unto them, The Son of man is delivered into the hands of men, and they shall kill him; and after that he is killed, he shall rise the third day.
9:32 Koma iwo sadazindikira mawuwo, nawopa kumfunsa Iye.	9:32 But they understood not that saying, and were afraid to ask him.
9:33 Ndipo Iye anadza ku Kaperna; ndipo pamene adakhala m'nyumba, Iye adawafunsa, Mudali kutsutsana chiyani panjira?	9:33 And he came to Capernaum: and being in the house he asked them, What was it that ye disputed among yourselves by the way?

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
9:34 Koma iwo adakhala chete; pakuti adatsutsana wina ndi mzake panjira kuti, wamkulu ndani?	9:34 But they held their peace: for by the way they had disputed among themselves, who should be the greatest.
9:35 Ndipo m'mene adakhala pansi adayitana khumi ndi awiriwo; nanena nawo, Ngati munthu afuna kukhala woyamba, akhale wa kuthungo wa onse, ndi mtumiki wa onse.	9:35 And he sat down, and called the twelve, and saith unto them, If any man desire to be first, the same shall be last of all, and servant of all.
9:36 Ndipo adatenga kamwana, nakayika pakati pawo, ndipo pamene adakayangata m'manja, ananena nawo,	9:36 And he took a child, and set him in the midst of them: and when he had taken him in his arms, he said unto them,
9:37 Munthu aliyense amene adzalandira kamodzi ka tiana totere chifukwa cha dzina langa, adzalandira Ine; ndipo yense amene adzalandira Ine, salandira Ine, koma Iye amene adandituma Ine.	9:37 Whosoever shall receive one of such children in my name, receiveth me: and whosoever shall receive me, receiveth not me, but him that sent me.
9:38 Ndipo Yohane adamuyankha Iye, nati: Mpulumutsi, tidawona munthu alikutulutsa ziwanda m'dzina lanu; ndipo tidamletsa, chifukwa sadali kutsata ife.	9:38 And John answered him, saying, Master, we saw one casting out devils in thy name, and he followeth not us: and we forbad him, because he followeth not us.
9:39 Koma Yesu adati, Musamamletsa iye; pakuti palibe munthu adzachita chozizwa m'dzina langa, nadzakhoza msanga kundinenera Ine zoyipa.	9:39 But Jesus said, Forbid him not: for there is no man which shall do a miracle in my name, that can lightly speak evil of me.
9:40 Pakuti iye wosatsutsana ndi ife ali kumbali yathu.	9:40 For he that is not against us is on our part.
9:41 Pakuti munthu aliyense adzakumwetsani inu chikho cha madzi m'dzina langa chifukwa muli ake a Khristu, indetu ndinena ndi inu, kuti iye sadzataya konse mphotho yake.	9:41 For whosoever shall give you a cup of water to drink in my name, because ye belong to Christ, verily I say unto you, he shall not lose his reward.
9:42 Ndipo yense amene adzalakwitsa kamodzi katiana timeneto takukhulupirira Ine, kuli kwabwino kwa iye makamaka kuti mwala waukulu wa mphero ukolowekedwe m'khosi mwake, naponyedwe m'nyanja.	9:42 And whosoever shall offend one of these little ones that believe in me, it is better for him that a millstone were hanged about his neck, and he were cast into the sea.
9:43 Ndipo ngati dzanja lako likulakwitsa iwe, ulidule: n'kwabwino kwa iwe kulowa m'moyo wopunduka dzanja, koposa kukhala ndi manja ako awiri ndi kulowa m'gehena, wa moto umene sudzakhoza kuzimitsidwa	9:43 And if thy hand offend thee, cut it off: it is better for thee to enter into life maimed, than having two hands to go into hell, into the fire that never shall be quenched:
9:44 Kumene mphutsi yawo siyifa, ndipo moto suzimitsidwa.	9:44 Where their worm dieth not, and the fire is not quenched.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
9:45 Ndipo ngati phazi likulakwitsa, ulidule; kulowa iwe m`moyo wopunduka mwendo, kuli kwabwino kuposa ndi kukhala ndi mapazi ako awiri ndi kuponyedwa m'gehena wa moto umene sudzakhoza kuzimitsidwa.	9:45 And if thy foot offend thee, cut it off: it is better for thee to enter halt into life, than having two feet to be cast into hell, into the fire that never shall be quenched:
9:46 Kumene mphutsi yawo simafa ndiponso moto suzimitsidwa.	9:46 Where their worm dieth not, and the fire is not quenched.
9:47 Ndipo ngati diso lako likulakwitsa ulikolowole; kulowa iwe mu Ufumu wa Mulungu ndi diso limodzi kuli kwabwino koposa ndi kukhala ndi maso awiri ndi kuponyedwa m'gehena wa moto.	9:47 And if thine eye offend thee, pluck it out: it is better for thee to enter into the kingdom of God with one eye, than having two eyes to be cast into hell fire:
9:48 Kumeneko mphutsi yawo siyikufa, ndipo moto suzimitsidwa.	9:48 Where their worm dieth not, and the fire is not quenched.
9:49 Pakuti onse adzathiridwa ndi mchere wa moto, ndi nsembe ili yonse idzathiridwa ndi m'chere.	9:49 For every one shall be salted with fire, and every sacrifice shall be salted with salt.
9:50 Mchere ndi wabwino; koma ngati mchere usukuluka, mudzaukoleretsa ndi chiyani? Khalani nawo mchere mwa inu nokha, ndipo khalani ndi mtendere wina ndi mzake.	9:50 Salt is good: but if the salt have lost his saltness, wherewith will ye season it? Have salt in yourselves, and have peace one with another.
<b>Mark 10</b>	<b>Mark 10</b>
10:1 Ndipo adanyamuka Iye kumeneko, nadza ku malire a ku Yudeya ndi kutsidya lija la Yordano; ndipo adasonkhananso kwa Iye anthu; ndipo monga adazolowera, adawaphunzitsanso.	10:1 And he arose from thence, and cometh into the coasts of Judaea by the farther side of Jordan: and the people resort unto him again; and, as he was wont, he taught them again.
10:2 Ndipo anadza kwa Iye Afarisi, adamfunsa Iye: kodi nkololedwa kuti munthu achotse mkazi wake? kumuyesa Iye.	10:2 And the Pharisees came to him, and asked him, Is it lawful for a man to put away his wife? tempting him.
10:3 Ndipo Iye adayankha nati kwa iwo, Kodi Mose adakulamulirani inu chiyani?	10:3 And he answered and said unto them, What did Moses command you?
10:4 Ndipo adati Mose adalola kulembera kalata wachilekaniro, ndi kumchotsa iye.	10:4 And they said, Moses suffered to write a bill of divorcement, and to put her away.
10:5 Ndipo Yesu adayankha nati kwa iwo, Chifukwa cha kuuma kwa mitima yanu adakulemberani lamulo ili.	10:5 And Jesus answered and said unto them, For the hardness of your heart he wrote you this precept.
10:6 Koma kuyambira pa chiyambi cha chilengedwe Mulungu adawapanga iwo mwamuna ndi mkazi.	10:6 But from the beginning of the creation God made them male and female.
10:7 Pachifukwa ichi mwamuna adzasiya atate wake ndi amayi ake, ndipo adzaphatikizana ndi mkazi wake;	10:7 For this cause shall a man leave his father and mother, and cleave to his wife;

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
10:8 Ndipo awiriwo adzakhala thupi limodzi: kotero kuti salinso awiri, koma thupi limodzi.	10:8 And they twain shall be one flesh: so then they are no more twain, but one flesh.
10:9 Chifukwa chake chimene Mulungu adachimanga pamodzi, asachilekenitse munthu.	10:9 What therefore God hath joined together, let not man put asunder.
10:10 Ndipo m'nyumba wophunzira adamfunsanso za chinthu ichi.	10:10 And in the house his disciples asked him again of the same matter.
10:11 Ndipo Iye adanena nawo, munthu ali yense akachotsa mkazi wake, nakakwatira wina, achita chigololo kulakwira mkaziyo.	10:11 And he saith unto them, Whosoever shall put away his wife, and marry another, committeth adultery against her.
10:12 Ndipo ngati mkazi akachotsa mwamuna wake, nakwatiwa ndi wina, achita chigololo iyeyu.	10:12 And if a woman shall put away her husband, and be married to another, she committeth adultery.
10:13 Ndipo adadza nato kwa Iye tiana, kuti atikhudze: ndipo wophunzira ake adawadzudzula iwo amene adadza nato.	10:13 And they brought young children to him, that he should touch them: and his disciples rebuked those that brought them.
10:14 Koma pamene Yesu adawona adakwiya kwambiri, ndipo adati kwa iwo, Lolani tiana tidze kwa Ine; musatiletse; pakuti Ufumu wa Mulungu uli wa totere.	10:14 But when Jesus saw it, he was much displeased, and said unto them, Suffer the little children to come unto me, and forbid them not: for of such is the kingdom of God.
10:15 Indetu ndinena ndi inu, munthu ali yense wosalandira Ufumu wa Mulungu ngati kamwana, sadzalowamo konse.	10:15 Verily I say unto you, Whosoever shall not receive the kingdom of God as a little child, he shall not enter therein.
10:16 Ndipo Iye adatiyangata ndi manja ake, natidalitsa, ndi kuyika manja ake pa ito.	10:16 And he took them up in his arms, put his hands upon them, and blessed them.
10:17 Ndipo pamene Iye adatuluka kutsata njira, adamthamangira m`modzi wolamulira, namgwadira Iye, namfunsu, Mphunzitsi wabwino, ndizichita chiyani kuti ndilandire moyo wosatha?	10:17 And when he was gone forth into the way, there came one running, and kneeled to him, and asked him, Good Master, what shall I do that I may inherit eternal life?
10:18 Ndipo Yesu adati kwa iye, Unditcha Ine wabwino bwanji? Palibe wabwino koma m`modzi ndiye Mulungu.	10:18 And Jesus said unto him, Why callest thou me good? there is none good but one, that is, God.
10:19 Udziwa malamulo usachite chigololo, usaphe, usabe, usachite umboni wonama, usanyenge, lemekeza atate wako ndi amako.	10:19 Thou knowest the commandments, Do not commit adultery, Do not kill, Do not steal, Do not bear false witness, Defraud not, Honour thy father and mother.
10:20 Ndipo iye adayankha nati kwa Iye, Mphunzitsi, zonsezi ndidazisunga kuyambira ndiri mwana.	10:20 And he answered and said unto him, Master, all these have I observed from my youth.



NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
10:21 Ndipo Yesu adamyang'ana, namkonda, nati kwa iye. Chinthu chimodzi chikusowa: pita gulitsa zonse uli nazo, nuzipereke kwa anthu aumphawi, ndipo chuma udzakhala nacho m'mwamba; ndipo ukadze kuno, senza mtanda unditsate Ine.	10:21 Then Jesus beholding him loved him, and said unto him, One thing thou lackest: go thy way, sell whatsoever thou hast, and give to the poor, and thou shalt have treasure in heaven: and come, take up the cross, and follow me.
10:22 Ndipo adakhumudwa ndi mawu awa, ndipo adachoka iye ali ndi chisoni; pakuti adali ndi chuma chambiri.	10:22 And he was sad at that saying, and went away grieved: for he had great possessions.
10:23 Ndipo Yesu adawunguzawunguza, nanena ndi wophunzira ake, Wokhala ndi chuma adzalowa mu Ufumu wa Mulungu mobvutika kwambiri!	10:23 And Jesus looked round about, and saith unto his disciples, How hardly shall they that have riches enter into the kingdom of God!
10:24 Ndipo wophunzirawo adazizwa ndithu ndi mawu ake. Koma Yesu adayankhanso nanena nawo, Ananu, nkobvuta ndithu kwa iwo akutama chuma kulowa mu Ufumu wa Mulungu!	10:24 And the disciples were astonished at his words. But Jesus answereth again, and saith unto them, Children, how hard is it for them that trust in riches to enter into the kingdom of God!
10:25 Ndi kwapafupi kuti ngamila ipyole pa diso la singano koposa kuti mwini chuma alowe mu Ufumu wa Mulungu.	10:25 It is easier for a camel to go through the eye of a needle, than for a rich man to enter into the kingdom of God.
10:26 Ndipo anadabwa koposa muyeso, nanena kwa iwo wokha, ndipo angathe kupulumuka ndani?	10:26 And they were astonished out of measure, saying among themselves, Who then can be saved?
10:27 Yesu adawayang'ana iwo nati, Sikutheka ndi anthu: koma kutheka ndi Mulungu pakuti ndi Mulungu zinthu zonse zitheka.	10:27 And Jesus looking upon them saith, With men it is impossible, but not with God: for with God all things are possible.
10:28 Petro adayamba kunena naye, Onani, ife tidasiya zonse, ndipo tidakutsatani Inu.	10:28 Then Peter began to say unto him, Lo, we have left all, and have followed thee.
10:29 Yesu adayankha nati, Indetu ndinena ndi inu ndithu, Palibe munthu adasiya nyumba, kapena abale, kapena alongo, kapena amayi, kapena atate kapena ana, kapena minda chifukwa cha Ine, ndi chifukwa cha Uthenga wabwino.	10:29 And Jesus answered and said, Verily I say unto you, There is no man that hath left house, or brethren, or sisters, or father, or mother, or wife, or children, or lands, for my sake, and the gospel's,
10:30 Koma adzalandira makumi khumi tsopano nthawi yino, nyumba, ndi abale ndi alongo ndi amayi, ndi ana, ndi minda, pamodzi ndi mazunzo; ndipo nthawi ili mkudza, moyo wosatha.	10:30 But he shall receive an hundredfold now in this time, houses, and brethren, and sisters, and mothers, and children, and lands, with persecutions; and in the world to come eternal life.
10:31 Koma ambiri akuyamba adzakhala akuthungo, ndi akuthungo adzakhala woyamba.	10:31 But many that are first shall be last; and the last first.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
10:32 Ndipo iwo adali m'njira ali kupita kumka ku Yerusalemu; ndipo Yesu adalikuwatsogolera; ndipo iwo adazizwa; ndipo pamene adalikumtsata adachita mantha. Ndipo Iye adatenganso khumi ndi awiriwo, nayamba kuwawuza zinthu zimene zidzamchitikira Iye.	10:32 And they were in the way going up to Jerusalem; and Jesus went before them: and they were amazed; and as they followed, they were afraid. And he took again the twelve, and began to tell them what things should happen unto him,
10:33 Nati, Tawonani, tikwera ku Yerusalemu; ndipo Mwana wa munthu adzaperekedwa kwa ansembe akulu ndi alembi; ndipo iwo adzamuweruza kuti ayenera imfa, nadzampereka Iye kwa anthu a mitundu.	10:33 Saying, Behold, we go up to Jerusalem; and the Son of man shall be delivered unto the chief priests, and unto the scribes; and they shall condemn him to death, and shall deliver him to the Gentiles:
10:34 Ndipo adzamnyoza Iye, nadzamthira malobvu, nadzamkwapula Iye, nadzamupha; ndipo patsiku la chitatu adzawukanso.	10:34 And they shall mock him, and shall scourge him, and shall spit upon him, and shall kill him: and the third day he shall rise again.
10:35 Ndipo anadza kwa Iye Yakobo ndi Yohane, ana a Zebedayo, nanena naye, Mphunzitsi, tifuna kuti mudzatichitire chimene chiri chonse tidzakhumba kwa Inu.	10:35 And James and John, the sons of Zebedee, come unto him, saying, Master, we would that thou shouldst do for us whatsoever we shall desire.
10:36 Ndipo Iye adati kwa iwo, Mufuna kuti ndidzakuchitireni inu chiyani?	10:36 And he said unto them, What would ye that I should do for you?
10:37 Ndipo iwo adati kwa Iye, Mutipatse ife kuti tikhale m'modzi kudzanja lanu lamanja, ndi wina kulamanzere, muulemerero wanu.	10:37 They said unto him, Grant unto us that we may sit, one on thy right hand, and the other on thy left hand, in thy glory.
10:38 Koma Yesu adati kwa iwo, Simudziwa chimene muchipempha. Mukhoza kodi kumwera chikho chimene ndimwera Ine? Kapena kubatizidwa ndi ubatizo umene ndidzabatizidwa nawo Ine?	10:38 But Jesus said unto them, Ye know not what ye ask: can ye drink of the cup that I drink of? and be baptized with the baptism that I am baptized with?
10:39 Ndipo adati kwa Iye, Tikhoza. Ndipo Yesu adati kwa iwo, Chikho chimene ndimwera Ine mudzamweradi; ndipo ubatizo ndibatizidwa nawo Ine, mudzabatizidwadi nawo.	10:39 And they said unto him, We can. And Jesus said unto them, Ye shall indeed drink of the cup that I drink of; and with the baptism that I am baptized withal shall ye be baptized:
10:40 Koma kukhala ku dzanja langa lamanja, kapena kulamanzere sikuli kwanga kupatsa; koma kudzapatsidwa kwa iwo amene kudakonzedweratu.	10:40 But to sit on my right hand and on my left hand is not mine to give; but it shall be given to them for whom it is prepared.
10:41 Ndipo pamene khumiwo adamva, adayamba kusasangalalitsidwa ndi Yakobo ndi Yohane.	10:41 And when the ten heard it, they began to be much displeased with James and John.
10:42 Ndipo Yesu adawayitana, nanena nawo, Mudziwa kuti iwo amene ayasedwa ambuye wa amitundu ya anthu amachita ufumu pa iwo; ndipo akulu awo amachita ulamuliro pa iwo.	10:42 But Jesus called them to him, and saith unto them, Ye know that they which are accounted to rule over the Gentiles exercise lordship over them; and their great ones exercise authority upon them.

<b>NYANJA</b>	<b>NEW INTERNATIONAL VERSION</b>
10:43 Koma mwa inu sikutero ayi; koma amene aliyense afuna kukhala wamkulu mwa inu adzakhala mtumiki wanu;	10:43 But so shall it not be among you: but whosoever will be great among you, shall be your minister:
10:44 Ndipo amene ali yense afuna kukhala woyamba mwa inu adzakhala mtumiki wa onse.	10:44 And whosoever of you will be the chiefest, shall be servant of all.
10:45 Pakuti ndithu, Mwana wa munthu sanadza kutumikiridwa, koma kutumikira, ndi kupereka moyo wake dipo la kwa ambiri.	10:45 For even the Son of man came not to be ministered unto, but to minister, and to give his life a ransom for many.
10:46 Ndipo iwo adafika ku Yeriko; ndipo m'mene Iye adalikutuluka mu Yeriko, ndi wophunzira ake, ndi khamu lalikulu la anthu, mwana wa Tineyu, Bartimeyu wakhungu adakhala pansu m'mbali mwa njira kumapempha.	10:46 And they came to Jericho: and as he went out of Jericho with his disciples and a great number of people, blind Bartimaeus, the son of Timaeus, sat by the highway side begging.
10:47 Ndipo pamene adamva kuti ndi Yesu wa ku Nazarete, adayamba kufuwula, ndi kunena, Yesu, Inu Mwana wa Davide, mundichitire ine chifundo.	10:47 And when he heard that it was Jesus of Nazareth, he began to cry out, and say, Jesus, thou son of David, have mercy on me.
10:48 Ndipo ambiri adamudzudzula kuti atonhole; koma makamaka adafuwulitsa kuti, Inu Mwana wa Davide, mundichitire chifundo.	10:48 And many charged him that he should hold his peace: but he cried the more a great deal, Thou son of David, have mercy on me.
10:49 Ndipo Yesu adayima nati, Mwitaneni. Ndipo adayitana munthu wakhunguyo, nanena naye, Limba mtima; nyamuka akuyitana.	10:49 And Jesus stood still, and commanded him to be called. And they call the blind man, saying unto him, Be of good comfort, rise; he calleth thee.
10:50 Ndipo iye adataya chofunda chake, nadzuka, nadza kwa Yesu.	10:50 And he, casting away his garment, rose, and came to Jesus.
10:51 Ndipo Yesu adayankha nati kwa iye, Ufuna kuti ndikuchitire chiyani? Ndipo munthu wakhunguyo adati kwa Iye, Ambuye, ndilandire kuwona kwanga.	10:51 And Jesus answered and said unto him, What wilt thou that I should do unto thee? The blind man said unto him, Lord, that I might receive my sight.
10:52 Ndipo Yesu adati kwa iye, Pita; chikhulupiriro chako chakupulumutsa iwe. Ndipo pomwepo adapenyanso; namtsata Yesu panjira.	10:52 And Jesus said unto him, Go thy way; thy faith hath made thee whole. And immediately he received his sight, and followed Jesus in the way.
<b>Mark 11</b>	<b>Mark 11</b>
11:1 Ndipo pamene iwo adayandikira ku Yerusalemu, ku Betefage ndi Betaniya, pa phiri la Azitona, adatuma awiri mwa wophunzira ake.	11:1 And when they came nigh to Jerusalem, unto Bethphage and Bethany, at the mount of Olives, he sendeth forth two of his disciples,

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
11:2 Ndipo adati kwa iwo, Pitani lowani m'mudzi wapandunji ndi inu; ndipo pomwepo pakulowamo mudzapeza mwana wa bulu womangidwa, amene palibe munthu adakhalapo kale lonse; m'masuleni iye, ndipo mubwere naye.	11:2 And saith unto them, Go your way into the village over against you: and as soon as ye be entered into it, ye shall find a colt tied, whereon never man sat; loose him, and bring him.
11:3 Ndipo munthu akati kwa inu, Mutero bwanji? Mukati, Ambuye akumfuna iye; ndipo pomwepo adzamtumiza kuno.	11:3 And if any man say unto you, Why do ye this? say ye that the Lord hath need of him; and straightway he will send him hither.
11:4 Ndipo adachoka napeza mwana wa bulu womangidwa pakhomo, pabwalo pamphambano pamene njira ziwiri zakumana, nam`masula iye.	11:4 And they went their way, and found the colt tied by the door without in a place where two ways met; and they loose him.
11:5 Ndipo ena woyima kumeneko adanena nawo, Muchita chiyani ndi kumasula mwana wa bulu?	11:5 And certain of them that stood there said unto them, What do ye, loosing the colt?
11:6 Ndipo adati kwa iwo monga momwe adawalamulira Yesu: ndipo adawalola iwo apite naye.	11:6 And they said unto them even as Jesus had commanded: and they let them go.
11:7 Ndipo anabwera naye mwana wa bulu kwa Yesu, nayika zobvala zawo pa iye, ndipo Iye adakhala pamenepo.	11:7 And they brought the colt to Jesus, and cast their garments on him; and he sat upon him.
11:8 Ndipo ambiri adayala zobvala zawo panjira; ndipo ena anadadula nthambi zamitengo naziyala njira.	11:8 And many spread their garments in the way: and others cut down branches off the trees, and strawed them in the way.
11:9 Ndipo iwo amene adatsogola ndi iwo ankamtsata, adafuwula nanena, Hosana wodalitsika Iye amene akudza m`dzina la Ambuye.	11:9 And they that went before, and they that followed, cried, saying, Hosanna; Blessed is he that cometh in the name of the Lord:
11:10 Wodalitsika ukhale ufumu wa atate wathu Davide umene ukudza dzina la Ambuye: Hosana m` Mwambamwamba.	11:10 Blessed be the kingdom of our father David, that cometh in the name of the Lord: Hosanna in the highest.
11:11 Ndipo Yesu adalowa mu Yerusalemu, ndipo nalowa m'kachisi; ndipo m'mene adawunguza zinthu zonse, popeza ndi madzulo adatuluka kupita ku Betaniya pamodzi ndi khumi ndi awiriwo.	11:11 And Jesus entered into Jerusalem, and into the temple: and when he had looked round about upon all things, and now the eventide was come, he went out unto Bethany with the twelve.
11:12 Ndipo m'mawa mwake, atatuluka ku Betaniya, Iye adamva njala.	11:12 And on the morrow, when they were come from Bethany, he was hungry:

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
11:13 Ndipo adawona mkuyu kutali, uli ndi masamba; ndipo anadza Iye mokondwera, kuti kapena akapezapo kanthu: ndipo m'mene adafikako adapeza palibe kanthu koma masamba wokha; pakuti sidali nyengo yake ya nkhuu.	11:13 And seeing a fig tree afar off having leaves, he came, if haply he might find any thing thereon: and when he came to it, he found nothing but leaves; for the time of figs was not yet.
11:14 Ndipo Yesu adayankha nanena ndi uwo, munthu sadzadyanso zipatso zako kuyambira tsopano mpaka nthawi zonse. Ndipo wophunzira ake adamva.	11:14 And Jesus answered and said unto it, No man eat fruit of thee hereafter for ever. And his disciples heard it.
11:15 Ndipo adafika iwo ku Yerusalemu; ndipo Yesu adalowa m'kachisi, nayamba kutulutsa wogulitsa ndi wogula malonda m'kachisimo, nagubuduza magome a wosinthana ndalama, ndi mipando ya wogulitsa nkhuu.	11:15 And they come to Jerusalem: and Jesus went into the temple, and began to cast out them that sold and bought in the temple, and overthrew the tables of the moneychangers, and the seats of them that sold doves;
11:16 Ndipo sadalole kuti munthu aliyense anyamule chotengera kupyola pakati pa kachisi.	11:16 And would not suffer that any man should carry any vessel through the temple.
11:17 Ndipo adaphunzitsa, nanena nawo, Sikudalembedwa kodi, Nyumba yanga idzatchedwa nyumba yopempheramo anthu a mitundu yonse? Koma inu mwayiyesa phanga la mbava.	11:17 And he taught, saying unto them, Is it not written, My house shall be called of all nations the house of prayer? but ye have made it a den of thieves.
11:18 Ndipo ansembe akulu ndi alembi adamva, nafunafuna njira yomuwonongera Iye; pakuti adamuwopa, chifukwa khamu lonse la anthu lidazizwa ndi chiphunzitsa chake.	11:18 And the scribes and chief priests heard it, and sought how they might destroy him: for they feared him, because all the people was astonished at his doctrine.
11:19 Ndipo pakufika madzulo adatuluka Iye mumzinda.	11:19 And when even was come, he went out of the city.
11:20 Ndipo m'mene adapitapo m'mawa mwake, adawona kuti mkuyu uja udawuma kuyambira kumizu.	11:20 And in the morning, as they passed by, they saw the fig tree dried up from the roots.
11:21 Ndipo Petro adakumbukira, nanena naye, Amphunzitsi, onani, wafota mkuyu uja mudautemberera.	11:21 And Peter calling to remembrance saith unto him, Master, behold, the fig tree which thou cursedst is withered away.
11:22 Ndipo Yesu adayankha nanena nawo, Khalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu.	11:22 And Jesus answering saith unto them, Have faith in God.
11:23 Indetu ndinena ndi inu, Kuti munthu aliyense akanena ndi phiri ili, Tanyamulidwa, nuponyedwe m'nyanja; wosakayika mumtima mwake, koma adzakhulupilira kuti chimene achinena chidzachitidwa, adzakhala nazo zonse zimene azinena.	11:23 For verily I say unto you, That whosoever shall say unto this mountain, Be thou removed, and be thou cast into the sea; and shall not doubt in his heart, but shall believe that those things which he saith shall come to pass; he shall have whatsoever he saith.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
11:24 Chifukwa chake ndinena ndi inu, Zinthu ziri zonse mukazikhumba pamene mupemphera, khulupirirani kuti mwazilandira, ndipo mudzakhala nazo.	11:24 Therefore I say unto you, What things soever ye desire, when ye pray, believe that ye receive them, and ye shall have them.
11:25 Ndipo pamene muyimilira ndi kupemphera, khululukirani ngati munthu wakulakwirani kanthu; kuti Atate wanunso ali kumwamba akhululukire inu zolakwa zanu.	11:25 And when ye stand praying, forgive, if ye have ought against any: that your Father also which is in heaven may forgive you your trespasses.
11:26 Koma ngati simukhulukira Atate wanu ali m'mwamba sadzakukhulukiranso inu zochimwa zanu.	11:26 But if ye do not forgive, neither will your Father which is in heaven forgive your trespasses.
11:27 Ndipo iwo anadzanso ku Yerusalemu; ndipo m'mene Iye adali kuyenda m'kachisi, adafika kwa Iye ansembe akulu, ndi alembi ndi akulu;	11:27 And they come again to Jerusalem: and as he was walking in the temple, there come to him the chief priests, and the scribes, and the elders,
11:28 Ndipo adati kwa iye, Izi muzichita ndi ulamuliro wotani? Kapena adakupatsani ndani ulamuliro uwu wochita izi?	11:28 And say unto him, By what authority doest thou these things? and who gave thee this authority to do these things?
11:29 Ndipo Yesu adayankha nati kwa iwo, Ndikufunsaninso inu funso limodzi, mundiyankhe Ine, ndipo ndidzakuwuzani ulamuliro umene ndichita nawo zinthu zimenezi.	11:29 And Jesus answered and said unto them, I will also ask of you one question, and answer me, and I will tell you by what authority I do these things.
11:30 Kodi ubatizo wa Yohane uchokera kumwamba kapena kwa anthu? Mundiyanke Ine.	11:30 The baptism of John, was it from heaven, or of men? answer me.
11:31 Ndipo adatsutsana mwa iwo wokha, nanena, Tikati, udachokera kumwamba; adzanena Iye, ndipo simudakhulupirira iye bwanji?	11:31 And they reasoned with themselves, saying, If we shall say, From heaven; he will say, Why then did ye not believe him?
11:32 Koma tikati kwa anthu; iwo adawopa anthuwo; pakuti anthu onse adamuyesa Yohane m'neneri ndithu.	11:32 But if we shall say, Of men; they feared the people: for all men counted John, that he was a prophet indeed.
11:33 Ndipo iwo adayankha nati kwa Yesu, Sitingakuwuzeni. Ndipo Yesu adanena nawo, Inenso sindikuwuzani ulamuliro umene ndichita nawo zinthu zimenezi	11:33 And they answered and said unto Jesus, We cannot tell. And Jesus answering saith unto them, Neither do I tell you by what authority I do these things.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
<b>Mark 12</b>	<b>Mark 12</b>
12:1 Ndipo Iye adayamba kuyankhula nawo m’mafanizo. Munthu wina adalima munda wa mphesa, nawuzunguniza ndi linga, nakumba moponderamo mphesa, namanga nsanja, naukongoletsa kwa wolima munda, napita kudziko lakutali.	12:1 And he began to speak unto them by parables. A certain man planted a vineyard, and set an hedge about it, and digged a place for the winefat, and built a tower, and let it out to husbandmen, and went into a far country.
12:2 Ndipo m’nyengo yake adatuma mtumiki kwa wolimawo, kuti akalandireko kwa wolimawo zipatso za m’unda wamphesa.	12:2 And at the season he sent to the husbandmen a servant, that he might receive from the husbandmen of the fruit of the vineyard.
12:3 Ndipo iwo adamgwira iye, nam’menya, namchotsa wopanda kanthu.	12:3 And they caught him, and beat him, and sent him away empty.
12:4 Ndipo adatumanso mtumiki wina kwa iwo; ndipo ameneyu adamponya miyala, namubvulaza m’mutu, namchotsa mwamanyazi wopanda kanthu.	12:4 And again he sent unto them another servant; and at him they cast stones, and wounded him in the head, and sent him away shamefully handled.
12:5 Ndipo adatuma wina; iyeyu adamupha; ndi ena ambiri; ena adawamenya, ndi ena adawapha.	12:5 And again he sent another; and him they killed, and many others; beating some, and killing some.
12:6 Adatsalira m’modzi, ndiye mwana wake wokonedwa; potsiriza adamtuma iye kwa iwo, nanena, Adzamchitira ulemu mwana wanga.	12:6 Having yet therefore one son, his wellbeloved, he sent him also last unto them, saying, They will reverence my son.
12:7 Koma wolima ajawo, adanena mwa iwo wokha, Ameneyu ndiye wolowa nyumba; tiyeni timuphe iye, ndipo mundawu udzakhala wathu.	12:7 But those husbandmen said among themselves, This is the heir; come, let us kill him, and the inheritance shall be ours.’
12:8 Ndipo adamantenga namupha iye, namtaya kunja kwa munda.	12:8 And they took him, and killed him, and cast him out of the vineyard.
12:9 Kodi pamenepo mwini munda adzachita chiyani? Adzafika, nadzawononga wolimawo, nadzapereka mundawo kwa ena.	12:9 What shall therefore the lord of the vineyard do? he will come and destroy the husbandmen, and will give the vineyard unto others.
12:10 Kodi simudawerenga ngakhale lembo ili; Mwala umene adawukana womanga nyumba, womwewu udayesedwa mutu wa pangodya.	12:10 And have ye not read this scripture; The stone which the builders rejected is become the head of the corner:
12:11 Awa ndi machitidwe Ambuye, ndipo ali wozizwitsa m’maso mwathu?	12:11 This was the Lord's doing, and it is marvellous in our eyes?
12:12 Ndipo adayesa kuti amgwire Iye; koma adawopa anthu, pakuti adazindikira kuti Iye adakamba fanizo ili potsutsa iwo; ndipo adamsiya Iye, nachoka.	12:12 And they sought to lay hold on him, but feared the people: for they knew that he had spoken the parable against them: and they left him, and went their way.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
12:13 Ndipo adatuma kwa Iye ena wa Afarisi ndi a Herode, kuti akamkole Iye m'kuyankhula kwake.	12:13 And they send unto him certain of the Pharisees and of the Herodians, to catch him in his words.
12:14 Ndipo pamene adafika, adanena naye, Mphunzitsi, tidziwa kuti muli wowona, ndipo simusamala munthu pakuti simuyang'ana nkhope ya munthu, koma muphunzitsa njira ya Mulungu mowona: nkuloleka kodi kupereka msonkho kwa Kaisara, kapena ayi?	12:14 And when they were come, they say unto him, Master, we know that thou art true, and carest for no man: for thou regardest not the person of men, but teachest the way of God in truth: Is it lawful to give tribute to Caesar, or not?
12:15 Kodi tipereke kapena tisapereke? Koma Iye podziwa chinyengo chawo, adati kwa iwo, Mundiyeserani? Nditengereni khobiri latheka, kuti ndiliwone.	12:15 Shall we give, or shall we not give? But he, knowing their hypocrisy, said unto them, Why tempt ye me? bring me a penny, that I may see it.
12:16 Ndipo adalitenga. Ndipo adati kwa iwo, Chithunzi ichi, ndi chilembo chake ziri za yani? Ndipo adati kwa Iye, za Kaisara.	12:16 And they brought it. And he saith unto them, Whose is this image and superscription? And they said unto him, Caesar's.
12:17 Ndipo Yesu poyankha adati kwa iwo, Perekani zake za Kaisara kwa Kaisara, ndi zake za Mulungu kwa Mulungu. Ndipo adazizwa naye.	12:17 And Jesus answering said unto them, Render to Caesar the things that are Caesar's, and to God the things that are God's. And they marvelled at him.
12:18 Ndipo anadza kwa Iye Asaduki amene amanena kuti palibe kuwuka kwa akufa; ndipo adamfunsa Iye, nanena	12:18 Then come unto him the Sadducees, which say there is no resurrection; and they asked him, saying,
12:19 Mphunzitsi, Mose adatilemba ife kuti, Akafa m'bale wake wa munthu, nasiya mkazi, wosasiyapo mwana, m'bale wake atenge mkazi wake namuukitsire mbale wakeyo mbewu.	12:19 Master, Moses wrote unto us, If a man's brother die, and leave his wife behind him, and leave no children, that his brother should take his wife, and raise up seed unto his brother.
12:20 Adalipo abale asanu ndi awiri; woyamba adakwatira mkazi, nafa, wosasiya mbewu;	12:20 Now there were seven brethren: and the first took a wife, and dying left no seed.
12:21 Ndipo wachiwiri adamkwatira iye nafa, wosasiya mbewu; ndipo wachitatunso adatero momwemo;	12:21 And the second took her, and died, neither left he any seed: and the third likewise.
12:22 Ndipo asanu ndi awiriwo adakhala naye ndipo sadasiya mbewu. Potsiriza pake pa onse mkaziyo adafanso.	12:22 And the seven had her, and left no seed: last of all the woman died also.
12:23 Chotero pakuwuka kwa akufa adzakhala mkazi wa yani wa iwowa? Pakuti asanu ndi awiriwo adamuyesa mkazi wawo.	12:23 In the resurrection therefore, when they shall rise, whose wife shall she be of them? for the seven had her to wife.
12:24 Ndipo Yesu poyankha adati, simusochera nanga mwa ichi, popeza mulibe kudziwa malembo, kapena mphamvu yake ya Mulungu?	12:24 And Jesus answering said unto them, Do ye not therefore err, because ye know not the scriptures, neither the power of God?



NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
12:25 Pakuti pamene adzawuka kwa akufa, sakwatira, kapena sakwatiwa, koma akhala ngati angelo akumwamba.	12:25 For when they shall rise from the dead, they neither marry, nor are given in marriage; but are as the angels which are in heaven.
12:26 Koma za akufa, kuti adzaukitsidwa simudawerenga m’buku la Mose kodi, momwe adalikuthengo, kuti Mulungu adati kwa iye, nanena, Ine ndine Mulungu wa Abrahamu, Isake ndi Mulungu wa Yakobo?	12:26 And as touching the dead, that they rise: have ye not read in the book of Moses, how in the bush God spake unto him, saying, I am the God of Abraham, and the God of Isaac, and the God of Jacob?
12:27 Iye sali Mulungu wa akufa, koma wa amoyo: musochera inu ndithu.	12:27 He is not the God of the dead, but the God of the living: ye therefore do greatly err.
12:28 Ndipo anadza m’modzi wa alembi, namva iwo alikufunsana pamodzi, ndipo podziwa kuti adawayankha bwino, adamfunsa Iye, Lamulo loyamba la onse ndi liti?	12:28 And one of the scribes came, and having heard them reasoning together, and perceiving that he had answered them well, asked him, Which is the first commandment of all?
12:29 Ndipo Yesu adamuyankha iye, Kuti lamulo loyamba la onse ndi ili, Mvera, Israyeli; Ambuye Mulungu wathu ndiye m’modzi.	12:29 And Jesus answered him, The first of all the commandments is, Hear, O Israel; The Lord our God is one Lord:
12:30 Ndipo uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru zako zonse, ndi mphamvu yako yonse: Ili ndi lamulo loyamba.	12:30 And thou shalt love the Lord thy God with all thy heart, and with all thy soul, and with all thy mind, and with all thy strength: this is the first commandment.
12:31 Ndipo lachiwiri ndi ili, uzikonda mzako monga uzikonda iwe mwini. Palibe lamulo lina loposa awa.	12:31 And the second is like, namely this, Thou shalt love thy neighbour as thyself. There is none other commandment greater than these.
12:32 Ndipo mlembiyo adati kwa Iye, Chabwino, mphunzitsi, mwanena zowona kuti ndi Mulungu m’modzi; ndipo palibe wina, koma Iye.	12:32 And the scribe said unto him, Well, Master, thou hast said the truth: for there is one God; and there is none other but he:
12:33 Ndipo kumkonda Iye ndi mtima wonse, ndi nzeru yonse, ndi mphamvu yonse, ndi kukonda mzako monga adzikonda mwini, ndiko kuposa nsembe zopsereza zamphumphu zonse, ndi nsembe zophedwa.	12:33 And to love him with all the heart, and with all the understanding, and with all the soul, and with all the strength, and to love his neighbour as himself, is more than all whole burnt offerings and sacrifices.
12:34 Ndipo Yesu pakuwona adayankha ndi nzeru adati kwa iye, Suli kutali ndi Ufumu wa Mulungu. Ndipo palibe munthu adalimbanso mtima kumfunsa Iye ndithu.	12:34 And when Jesus saw that he answered discreetly, he said unto him, Thou art not far from the kingdom of God. And no man after that durst ask him any question.
12:35 Ndipo Yesu adayankha nati, pamene adali kuphunzitsa m’kachisi, Bwanji alembi akunena kuti Khristu ndiye mwana wa Davide?	12:35 And Jesus answered and said, while he taught in the temple, How say the scribes that Christ is the son of David?

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
12:36 Pakuti Davide mwini yekha adati mwa Mzimu Woyera, Ambuye adati kwa Ambuye wanga, khala ku dzanja langa lamanja, kufikira nditawayika adani ako popondapo mapazi ako.	12:36 For David himself said by the Holy Ghost, The Lord said to my Lord, Sit thou on my right hand, till I make thine enemies thy footstool.
12:37 Chomwecho Davide mwini yekha amtchula Iye Ambuye; ndipo ali mwana wake bwanji? Ndipo anthu a makamuwo adakondwa kumva Iye.	12:37 David therefore himself calleth him Lord; and whence is he then his son? And the common people heard him gladly.
12:38 Ndipo Iye adati kwa iwo m'chiphunzitsio chake, Chenjerani ndi alembi, akonda kubvala miyinjiro nakonda kulandira ulemu m'misika.	12:38 And he said unto them in his doctrine, Beware of the scribes, which love to go in long clothing, and love salutations in the marketplaces,
12:39 Nakhala nayo mipando yaulemu m'sunagoge, ndi malo a ulemu pamaphwando;	12:39 And the chief seats in the synagogues, and the uppermost rooms at feasts:
12:40 Amenewa alusira nyumba za akazi a masiye, napemphera monyenga mawu ambiri, amenewa adzalandira kulanga koposa.	12:40 Which devour widows' houses, and for a pretence make long prayers: these shall receive greater damnation.
12:41 Ndipo Yesu adakhala panso pandunji pa mosungiramo zopereka, napenya momwe anthu adali kuponyera ndalama mosungiramo; ndipo eni chuma ambiri adaponyamo zambiri.	12:41 And Jesus sat over against the treasury, and beheld how the people cast money into the treasury: and many that were rich cast in much.
12:42 Ndipo anadza mkazi wamasiye waumphawi, ndipo iye adaponyamo tindalama tiwiri tating'ono topanga khobiri limodzi.	12:42 And there came a certain poor widow, and she threw in two mites, which make a farthing.
12:43 Ndipo adayitana wophunzira ake, nati kwaiwo, ndithu ndinena ndi inu, mkazi wamasiye amene waumphawi adaponya zambiri koposa onse woponya mosungiramo:	12:43 And he called unto him his disciples, and saith unto them, Verily I say unto you, That this poor widow hath cast more in, than all they which have cast into the treasury:
12:44 Pakuti onse adaponyamo mwa zochuluka zawo; koma iye adaponya mwa kusowa kwake zonse adali nazo, inde ndi za moyo wake wonse.	12:44 For all they did cast in of their abundance; but she of her want did cast in all that she had, even all her living.
<b>Mark 13</b>	<b>Mark 13</b>
13:1 Ndipo pamene Iye adalikutuluka m'kachisi m'modzi wa wophunzira ake adanena kwa Iye, Mphunzitsi, onani, miyala yotere ndi nyumba yotere.	13:1 And as he went out of the temple, one of his disciples saith unto him, Master, see what manner of stones and what buildings are here!
13:2 Ndipo Yesu poyankha adati kwa iye, Kodi waona nyumba izi zazikulu? Sudzasiyidwa pano mwala umodzi pamwamba pa umzake, umene sudzagwetsedwa panso.	13:2 And Jesus answering said unto him, Seest thou these great buildings? there shall not be left one stone upon another, that shall not be thrown down.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
13:3 Ndipo pamene Iye adakhala pa phiri la Azitona, popenyana ndi kachisi adamfunsa Iye mseri Petro, ndi Yakobo, ndi Yohane ndi Andreyana kuti,	13:3 And as he sat upon the mount of Olives over against the temple, Peter and James and John and Andrew asked him privately,
13:4 Tiwuzeni zinthu izi zidzachitika liti? Ndi chotani chizindikiro chake pamene zinthu izi zonse zidzakwaniritsidwa?	13:4 Tell us, when shall these things be? and what shall be the sign when all these things shall be fulfilled?
13:5 Ndipo Yesu powayankha iwo adanena nawo, Chenjerani kuti munthu asakusocheretseni:	13:5 And Jesus answering them began to say, Take heed lest any man deceive you:
13:6 Pakuti ambiri adzafika m'dzina langa, nadzanena, Ine ndine Khristu; nadzasocheretsa ambiri.	13:6 For many shall come in my name, saying, I am Christ; and shall deceive many.
13:7 Ndipo pamene mudzamva za nkondo ndi mbiri zake za nkondo, musamadera nkawa: ziyenera kuchitika izi; koma sichidafike chimaliziro.	13:7 And when ye shall hear of wars and rumours of wars, be ye not troubled: for such things must needs be; but the end shall not be yet.
13:8 Pakuti mtundu wa anthu udzawukirana ndi mtundu wina, ndipo ufumu ndi ufumu wina umzake; padzakhala zibvomerezi m'malo osiyanasiyana; padzakhala njala ndi mabvuto; Izi ndi zoyambira za zowawa.	13:8 For nation shall rise against nation, and kingdom against kingdom: and there shall be earthquakes in divers places, and there shall be famines and troubles: these are the beginnings of sorrows.
13:9 Koma inu mudziyang'anire inu nokha; pakuti adzakuperekani inu kwa akulu a milandu; ndipo adzakukwapulani m'masunagoge mwao; ndipo pamaso pa akazembe ndi mafumu mudzayimilira chifukwa cha Ine, kukhala umboni kwa iwo.	13:9 But take heed to yourselves: for they shall deliver you up to councils; and in the synagogues ye shall be beaten: and ye shall be brought before rulers and kings for my sake, for a testimony against them.
13:10 Ndipo Uthenga wabwino uyenera uyambe kulalikidwa kwa anthu a mitundu yonse.	13:10 And the gospel must first be published among all nations.
13:11 Ndipo pamene adzapita nanu kumlandu, nadzakuperekani, musade nkawa chimene mudzayankhula; kapena kulingalira koma chimene chidzapatsidwa kwa inu ora lomwelo, muchiyankhule; pakuti woyankhula si inu, koma Mzimu Woyera.	13:11 But when they shall lead you, and deliver you up, take no thought beforehand what ye shall speak, neither do ye premeditate: but whatsoever shall be given you in that hour, that speak ye: for it is not ye that speak, but the Holy Ghost.
13:12 Ndipo m'bale adzapereka m'bale wake kuti aphedwe, ndi atate mwana wake; ndi ana adzawukirana ndi akuwabala nadzawaphetsa.	13:12 Now the brother shall betray the brother to death, and the father the son; and children shall rise up against their parents, and shall cause them to be put to death.
13:13 Ndipo mudzadedwa ndi anthu onse chifukwa cha dzina langa; koma iye wopilira kufikira chimaliziro, yemweyo adzapulumutsidwa.	13:13 And ye shall be hated of all men for my name's sake: but he that shall endure unto the end, the same shall be saved.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
13:14 Ndipo pamene mudzawona chonyansa cha kupululutsa chimene chidayankhulidwa ndi Danieli m`neneri (iye amene awerenga azindikire ) chitayima pomwe sichiyenera kuyima pamenepo iwo ali mu Yudeya athawire ku mapiri:	13:14 But when ye shall see the abomination of desolation, spoken of by Daniel the prophet, standing where it ought not, (let him that readeth understand,) then let them that be in Judaea flee to the mountains:
13:15 Ndipo iye amene ali pamwamba pa denga asatsike, kapena asalowe kukatulutsa kanthu m`nyumba mwake;	13:15 And let him that is on the housetop not go down into the house, neither enter therein, to take any thing out of his house:
13:16 Ndi iye amene ali kumunda asabwere kudzatenga malaya ake.	13:16 And let him that is in the field not turn back again for to take up his garment.
13:17 Koma tsoka kwa iwo wokhala ndi mwana ndi iwo akuyamwitsa m`masiku amenewo!	13:17 But woe to them that are with child, and to them that give suck in those days!
13:18 Ndipo pempherani kuti kuthawa kwanu kusadzakhale m`nyengo yozizira.	13:18 And pray ye that your flight be not in the winter.
13:19 Pakuti masiku amenewo padzakhala chisautso, chonga sichidakhalepo chimzake kuyambira chiyambi cha chilengedwe chimene Mulungu adachilenga ndi kufikira tsopano, ndipo sichidzakhalanso nthawi zonse.	13:19 For in those days shall be affliction, such as was not from the beginning of the creation which God created unto this time, neither shall be.
13:20 Ndipo Ambuye akadapanda kufupikitsa masikuwo, sakadapulumuka munthu m`modzi yense; koma chifukwa cha wosankhidwa amene adawasankha, adafupikitsa masikuwo.	13:20 And except that the Lord had shortened those days, no flesh should be saved: but for the elect's sake, whom he hath chosen, he hath shortened the days.
13:21 Ndipo pamenepo ngati munthu wina anena kwa inu, Onani Khristu ali pano; kapena Onani, ali uko; musakhulupirire;	13:21 And then if any man shall say to you, Lo, here is Christ; or, lo, he is there; believe him not:
13:22 Pakuti adzawuka Akhristu wonyenga ndi aneneri wonyenga, ndipo adzachita zizindikiro ndi zozizwitsa, kuti akasoheretse, ngati n`kuthaka, wosankhidwa omwe.	13:22 For false Christs and false prophets shall rise, and shall shew signs and wonders, to seduce, if it were possible, even the elect.
13:23 Koma inu chenjerani; Onani, ndakuwuziranitu zinthu zonse, zisadafike.	13:23 But take ye heed: behold, I have foretold you all things.
13:24 Koma m`masiku amenewo, chitatha chisautso chimenecho, dzuwa lidzadetsedwa ndi mwezi sudzapatsa kuwunika kwake.	13:24 But in those days, after that tribulation, the sun shall be darkened, and the moon shall not give her light,
13:25 Ndipo nyenyezi zidzagwa kuchokera m`mwamba ndi mphamvu ziri m`mwamba zidzagwedezeka.	13:25 And the stars of heaven shall fall, and the powers that are in heaven shall be shaken.
13:26 Ndipo pamenepo adzawona Mwana wa Munthu ali mkudza m`mitambo ndi mphamvu yayikulu, ndi ulemerero.	13:26 And then shall they see the Son of man coming in the clouds with great power and glory.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
13:27 Ndipo pamenepo adzatumo angelo ake, nadzasonkhanitsa wosankhidwa ake wochokera ku mphepo zinayi, kuyambira ku malekezero ake a dziko lapansi, ndi kufikira ku malekezero a thambo.	13:27 And then shall he send his angels, and shall gather together his elect from the four winds, from the uttermost part of the earth to the uttermost part of heaven.
13:28 Tsopano phunzirani fanizo la mtengo wa mkuyu; pamene pafika kuti nthambi yake yanthete, ndipo akaphuka masamba ake, muzindikira kuti layandikira dzinja.	13:28 Now learn a parable of the fig tree; When her branch is yet tender, and putteth forth leaves, ye know that summer is near:
13:29 Chomwecho inunso, pamene mudzawona zinthu izi zili kuchitika, zindikirani kuti ali pafupi, inde pakhomo.	13:29 So ye in like manner, when ye shall see these things come to pass, know that it is nigh, even at the doors.
13:30 Indetu ndinena ndi inu, Mbadwo uno sudzapita kufikira zinthu izi zonse zitachitika.	13:30 Verily I say unto you, that this generation shall not pass, till all these things be done.
13:31 Thambo ndi dziko lapansi zidzapita; koma mawu anga sadzapita.	13:31 Heaven and earth shall pass away: but my words shall not pass away.
13:32 Koma za tsikulo, kapena nthawi yake sadziwa munthu, angakhale angelo m'mwamba, angakhale Mwana, koma Atate ndiye adziwa.	13:32 But of that day and that hour knoweth no man, no, not the angels which are in heaven, neither the Son, but the Father.
13:33 Chenjerani, dikirani, pempherani: pakuti simudziwa nthawi yake.	13:33 Take ye heed, watch and pray: for ye know not when the time is.
13:34 Pakuti Mwana wa Munthu ali monga ngati munthu wa pa ulendo, amene adachoka kunyumba kwake, nawapatsa atumiki ake ulamuliro, kwa munthu aliyense ntchito yake, nalamulira wapakhomo adikire.	13:34 For the Son of Man is as a man taking a far journey, who left his house, and gave authority to his servants, and to every man his work, and commanded the porter to watch.
13:35 Chifukwa chake dikirani, pakuti simudziwa inu nthawi yake yobwera mwini nyumba, kapena madzulo, kapena pakati pa usiku, kapena pakulira tambala, kapena mamawa;	13:35 Watch ye therefore: for ye know not when the master of the house cometh, at even, or at midnight, or at the cockcrowing, or in the morning:
13:36 Kuti angabwere modzidzimutsa nadzakupezani muli mtulo.	13:36 Lest coming suddenly he find you sleeping.
13:37 Ndipo chimene ndinena ndi inu ndinena kwa onse, Dikirani.	13:37 And what I say unto you I say unto all, Watch.
<b>Mark 14</b>	<b>Mark 14</b>
14:1 Ndipo popita masiku awiri kudali phwando la Paskha ndi mikate yopanda chotupitsa; ndipo ansembe akulu ndi alembi adafunafuna momwe angamgwirirre momchenjerera, ndi kumupha;	14:1 After two days was the feast of the passover, and of unleavened bread: and the chief priests and the scribes sought how they might take him by craft, and put him to death.
14:2 Koma adati, paphwando ayi, kuti pangakhale phokoso chipolowe cha anthu.	14:2 But they said, Not on the feast day, lest there be an uproar of the people.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
14:3 Ndipo pakukhala Iye ku Betaniya m’nyumba ya Simoni wakhate, m’mene adasayama kudya, anadzapo mkazi ali nayo nsupa ya alabasitala ya mafuta wonunkhira bwino a nardo weni weni a mtengo wapatali; naswa nsupayo, nawatsanulira pamutu pake.	14:3 And being in Bethany in the house of Simon the leper, as he sat at meat, there came a woman having an alabaster box of ointment of spikenard very precious; and she brake the box, and poured it on his head.
14:4 Koma adakhalako ena adabvutika mtima mwa iwo wokha, ndi kuti, Mafutawo atayidwa chifukwa ninji?	14:4 And there were some that had indignation within themselves, and said, Why was this waste of the ointment made?
14:5 Pakuti mafuta amene akadagulitsa makobiri oposa mazana atatu ndi mphambu zake, ndi kupatsa aumphawi. Ndipo adanyinyirika motsutsana ndi iye.	14:5 For it might have been sold for more than three hundred pence, and have been given to the poor. And they murmured against her.
14:6 Ndipo Yesu adati, Mulekeni, mumbvutirani? Wandichitira Ine ntchito yabwino.	14:6 And Jesus said, Let her alone; why trouble ye her? she hath wrought a good work on me.
14:7 Pakuti muli nawo aumphawi pamodzi ndi inu masiku onse, ndipo paliponse pamene mufuna mukhoza kuwachitira zabwino; koma Ine simuli nane masiku onse.	14:7 For ye have the poor with you always, and whensoever ye will ye may do them good: but me ye have not always.
14:8 Iye wachita chimene wakhoza; adandidzozeratu thupi langa ku kuyikidwa m’manda.	14:8 She hath done what she could: she is come aforehand to anoint my body to the burying.
14:9 Indetu ndinena ndi inu; paliponse pamene padzalalikidwa Uthenga Wabwino ku dziko lonse lapansi, ichinso chimene adachita mkazi uyu chidzanenedwa, chikhale chomkumbukira nacho.	14:9 Verily I say unto you, Wheresoever this gospel shall be preached throughout the whole world, this also that she hath done shall be spoken of for a memorial of her.
14:10 Ndipo Yudas Isikariyote, ndiye m’modzi wa khumi ndi awiriwo, adachoka napita kwa ansembe akulu, kuti akampereke Iye kwa iwo.	14:10 And Judas Iscariot, one of the twelve, went unto the chief priests, to betray him unto them.
14:11 Ndipo pamene iwo adamva, adasekera, nalonjezana naye kuti adzampatsa ndalama. Ndipo iye adafunafuna momwe angamperekere Iye bwino.	14:11 And when they heard it, they were glad, and promised to give him money. And he sought how he might conveniently betray him.
14:12 Ndipo tsiku loyamba la mikate yopanda chotupitsa, pamene amapha Paskha, wophunzira ake adanena naye, Mufuna tipite kuti, tikakonze mukadyereko Paskha?	14:12 And the first day of unleavened bread, when they killed the passover, his disciples said unto him, Where wilt thou that we go and prepare that thou mayest eat the passover?
14:13 Ndipo adatuma awiri wophunzira ake, nanena nawo, Lowani mu mzinda, ndipo mudzakomana ndi munthu wosenza mtsuko wa madzi; mumtsate iye;	14:13 And he sendeth forth two of his disciples, and saith unto them, Go ye into the city, and there shall meet you a man bearing a pitcher of water: follow him.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
14:14 Ndipo kumene adzalowako iye, munene naye mwini nyumba wabwino, Mphunzitsi anena, chiri kuti chipinda cha alendo m'menemo ndidzadyera Paskha ndi wophunzira anga?	14:14 And wheresoever he shall go in, say ye to the goodman of the house, The Master saith, Where is the guestchamber, where I shall eat the passover with my disciples?
14:15 Ndipo iye yekha adzakusonyezani chipinda, chapamwamba chachikulu choyalamo ndi chokonzedwa; ndipo m'menemo mutikonzere ife.	14:15 And he will shew you a large upper room furnished and prepared: there make ready for us.
14:16 Ndipo wophunzira adatuluka, nafika mu mzinda, napeza monga adati kwa iwo; ndipo adakonza Paskha.	14:16 And his disciples went forth, and came into the city, and found as he had said unto them: and they made ready the passover.
14:17 Ndipo madzulo adafika, Iye pamodzi ndi khumi ndi awiriwo.	14:17 And in the evening he cometh with the twelve.
14:18 Ndipo pamene iwo adakhala pansu ndi kudya, Yesu adati, Indetu ndinena ndi inu, m'modzi wa inu adzandipereka Ine, ndiye wakudya ndi Ine pamodzi.	14:18 And as they sat and did eat, Jesus said, Verily I say unto you, One of you which eateth with me shall betray me.
14:19 Ndipo iwo adayamba kukhala ndi chisoni, ndi kunena naye m'modzi m'modzi, kuti Ndine kodi? Ndipo wina adati kodi ndine?	14:19 And they began to be sorrowful, and to say unto him one by one, Is it I? and another said, Is it I?
14:20 Ndipo adati kwa iwo, Mmodzi wa khumi ndi awiriwo, ndiye wosunsa pamodzi ndi ine m'bale.	14:20 And he answered and said unto them, It is one of the twelve, that dipped with me in the dish.
14:21 Pakuti Mwana wa munthu amukadi; monga kwalembedwa za Iye; koma tsoka munthuyo amene apereka Mwana wa munthu! Kukadakhala kwabwino kwa munthu ameneyo akadakhala kuti sadabadwe.	14:21 The Son of man indeed goeth, as it is written of him: but woe to that man by whom the Son of man is betrayed! good were it for that man if he had never been born.
14:22 Ndipo pamene analikudya, Yesu adatenga mkate, ndipo pamene anadalitsa, adanyema, napereka kwa iwo, nati: Tengani, idyani, ili ndi thupi langa.	14:22 And as they did eat, Jesus took bread, and blessed, and brake it, and gave to them, and said, Take, eat: this is my body.
14:23 Ndipo adatenga chikho, ndipo pamene adayamika, adapereka kwa iwo, ndipo iwo onse adamweramo.	14:23 And he took the cup, and when he had given thanks, he gave it to them: and they all drank of it.
14:24 Ndipo Iye adati kwa iwo, Uwu ndi mwazi wanga wa pangano latsopano, wokhetsedwa chifukwa cha anthu ambiri.	14:24 And he said unto them, This is my blood of the new testament, which is shed for many.
14:25 Indetu ndinena kwa inu, sindidzamwanso chipatso cha mpesa, kufikira tsiku lijalo, limene ndidzamwa icho chatsopano mu Ufumu wa Mulungu.	14:25 Verily I say unto you, I will drink no more of the fruit of the vine, until that day that I drink it new in the kingdom of God.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
14:26 Ndipo atayimba nyimbo, adatuluka, napita ku phiri la Azitona.	14:26 And when they had sung an hymn, they went out into the mount of Olives.
14:27 Ndipo Yesu adati kwa iwo, mudzakhumudwa nonsenu usiku uno chifukwa cha Ine; pakuti kwalembedwa; Ndidzakantha m`busa, ndi nkhusa zidzabalalika.	14:27 And Jesus saith unto them, All ye shall be offended because of me this night: for it is written, I will smite the shepherd, and the sheep shall be scattered.
14:28 Komatu nditadzauka ndidzatsogolera inu ku Galileya.	14:28 But after that I am risen, I will go before you into Galilee.
14:29 Koma Petro adati kwa Iye, Angakhale adzakhumudwa onse komatu ine ayi.	14:29 But Peter said unto him, Although all shall be offended, yet will not I.
14:30 Ndipo Yesu adati kwa iye, Indetu ndinena ndi iwe, kuti lero, usiku uno, tambala asadalire kawiri udzandikana Ine katatu.	14:30 And Jesus saith unto him, Verily I say unto thee, That this day, even in this night, before the cock crow twice, thou shalt deny me thrice.
14:31 Koma iye adayankhula molimbitsa mawu kuti, Ngakhale ndidzafa nanu, sindidzakana Inu. Ndipo onsewo adatero.	14:31 But he spake the more vehemently, If I should die with thee, I will not deny thee in any wise. Likewise also said they all.
14:32 Ndipo iwo anadza ku malo dzina lake Getsemane; ndipo adanena kwa wophunzira ake, Bakhalani pano, kufikira ndikapemphera.	14:32 And they came to a place which was named Gethsemane: and he saith to his disciples, Sit ye here, while I shall pray.
14:33 Ndipo adatenga pamodzi ndi Iye Petro, ndi Yakobo, ndi Yohane, nayamba kudabwa kwambiri, ndi kulemedwa mtima ndithu.	14:33 And he taketh with him Peter and James and John, and began to be sore amazed, and to be very heavy;
14:34 Ndipo adati kwa iwo, Moyo wanga uli wa chisoni chambiri kufikira imfa. Bakhalani pano, nimudikire.	14:34 And saith unto them, My soul is exceeding sorrowful unto death: tarry ye here, and watch.
14:35 Ndipo Iye anapita m'tsogolo pang'ono, nagwa pansu, napemphera kuti ngati n'kutheka nthawi imeneyi indipitirire Ine.	14:35 And he went forward a little, and fell on the ground, and prayed that, if it were possible, the hour might pass from him.
14:36 Ndipo Iye adati, Abba, Atate, zinthu zonse zitheka ndi Inu, mundichotsere chikho ichi; komatu si chimene ndifuna Ine, koma chimene mufuna Inu.	14:36 And he said, Abba, Father, all things are possible unto thee; take away this cup from me: nevertheless not what I will, but what thou wilt.
14:37 Ndipo anadza nawapeza iwo ali m'tulo, nanena ndi Petro, Simoni, ugoni kodi? Ulibe mphamvu yakudikira ola limodzi kodi?	14:37 And he cometh, and findeth them sleeping, and saith unto Peter, Simon, sleepest thou? couldest not thou watch one hour?
14:38 Dikirani, pempherani, kuti mungalowe m'kuyesedwa; mzimutu ali wofuna, koma thupi liri lolefuka.	14:38 Watch ye and pray, lest ye enter into temptation. The spirit truly is ready, but the flesh is weak.
14:39 Ndipo adachokanso, napemphera, nanena mawu womwewo.	14:39 And again he went away, and prayed, and spake the same words.



NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
14:40 Ndipo anadzanso nawapeza ali m'tulo, pakuti maso awo adalemeradi; ndipo sadadziwe chomuyankha Iye.	14:40 And when he returned, he found them asleep again, (for their eyes were heavy,) neither wist they what to answer him.
14:41 Ndipo anadza kachitatu, nanena nawo, Gonani tsopano; nimupumule; chakwanira; yafika nthawi; onani Mwana wa munthu aperekedwa m'manja wa anthu wochimwa.	14:41 And he cometh the third time, and saith unto them, Sleep on now, and take your rest: it is enough, the hour is come; behold, the Son of man is betrayed into the hands of sinners.
14:42 Ukani, tidzipita; onani wondiperekayo ali pafupi.	14:42 Rise up, let us go; lo, he that betrayeth me is at hand.
14:43 Ndipo pomwepo Iye ali chiyankhulire, anadza Yudase, m'modzi wa khumi ndi awiriwo, ndipo pamodzi naye khamu la anthu, ali nawo malupanga ndi zibonga, wochokera kwa ansembe akulu ndi alembi ndi akulu.	14:43 And immediately, while he yet spake, cometh Judas, one of the twelve, and with him a great multitude with swords and staves, from the chief priests and the scribes and the elders.
14:44 Ndipo womperera Iye adawapatsa chizindikiro, nanena, Iye amene ndidzampsona, ndiyetu; mgwireni munke naye chisungire.	14:44 And he that betrayed him had given them a token, saying, Whomsoever I shall kiss, that same is he; take him, and lead him away safely.
14:45 Ndipo atafika, pomwepo anadza kwa Iye, nanena Mphunzitsi, mphunzitsi: nampsonetsa Iye.	14:45 And as soon as he was come, he goeth straightway to him, and saith, Master, master; and kissed him.
14:46 Ndipo adamthira manja, namgwira namtenga Iye.	14:46 And they laid their hands on him, and took him.
14:47 Ndipo m'modzi wina wa iwo woyimilira pamenepo, adasolola lupanga lake, nakantha mtumiki wa mkulu wa ansembe, namdula khutu lake.	14:47 And one of them that stood by drew a sword, and smote a servant of the high priest, and cut off his ear.
14:48 Ndipo Yesu adayankha nati kwa iwo, Kodi mwatuluka ndi malupanga ndi zibonga kundigwira Ine monga bava?	14:48 And Jesus answered and said unto them, Are ye come out, as against a thief, with swords and with staves to take me?
14:49 Masiku onse ndidali nanu m'kachisi ndiri kuphunzitsa, ndipo simudandigwire Ine; koma ichi chachitika kuti malembo akwaniritsidwe.	14:49 I was daily with you in the temple teaching, and ye took me not: but the scriptures must be fulfilled.
14:50 Ndipo iwo onse adamsiya Iye, nathawa.	14:50 And they all forsook him, and fled.
14:51 Ndipo m'nyamata wina adamtsata Iye, atafundira pathupi bafuta yekha kubisa umaliseche wake; ndipo anyamatawo adamuyimitsa Iye;	14:51 And there followed him a certain young man, having a linen cloth cast about his naked body; and the young men laid hold on him:
14:52 Ndipo iye adasiya bafutayo, nathawa wamaliseche.	14:52 And he left the linen cloth, and fled from them naked.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
14:53 Ndipo adamka naye Yesu kwa mkulu wa ansembe; ndipo adasonkhana kwa iye ansembe akulu onse ndi akulu a anthu, ndi alembi.	14:53 And they led Jesus away to the high priest: and with him were assembled all the chief priests and the elders and the scribes.
14:54 Ndipo Petro adamsata Iye kutali, kufikira kulowa m'bwalo la mkulu wa ansembe; ndipo adali kukhala pansu pamodzi ndi atumiki, ndi kuwotha moto.	14:54 And Peter followed him afar off, even into the palace of the high priest: and he sat with the servants, and warmed himself at the fire.
14:55 Ndipo ansembe akulu ndi akulu a milandu onse adafunafuna umboni womutsutsa nawo Yesu kuti amuphe Iye; koma sadaupeze.	14:55 And the chief priests and all the council sought for witness against Jesus to put him to death; and found none.
14:56 Pakuti ambiri adamchitira umboni wonama, ndipo umboni wawo sudalingane.	14:56 For many bare false witness against him, but their witness agreed not together.
14:57 Ndipo adanyamukapo ena, namchitira umboni wonama, nanena kuti,	14:57 And there arose certain, and bare false witness against him, saying,
14:58 Ife tidamumva Iye alikunena kuti Ine ndidzawononga kachisi uyu wopangidwa ndi manja, ndi masiku atatu ndidzamanga wina wosamangidwa ndi manja.	14:58 We heard him say, I will destroy this temple that is made with hands, and within three days I will build another made without hands.
14:59 Ndipo ngakhale momwemo umboni wawo sudafanane.	14:59 But neither so did their witness agree together.
14:60 Ndipo mkulu wa ansembe adanyamuka pakati, namfunsa Yesu, nanena, Suyankha kanthu kodi? Nchiyani ichi chimene awa alikuchitira umboni mokutsutsa Iwe.	14:60 And the high priest stood up in the midst, and asked Jesus, saying, Answerest thou nothing? what is it which these witness against thee?
14:61 Koma adakhala chete, osayankha kanthu. Mkulu wa ansembe adamfunsanso, nanena naye, Kodi Iwe ndiwe Khristu, Mwana wake wa Wodalitsika?	14:61 But he held his peace, and answered nothing. Again the high priest asked him, and said unto him, Art thou the Christ, the Son of the Blessed?
14:62 Ndipo Yesu adati, Ndine amene; ndipo mudzawona Mwana wa munthu alikukhala kudzanja lamanja la mphamvu, ndi kudza ndi mitambo yakumwamba.	14:62 And Jesus said, I am: and ye shall see the Son of man sitting on the right hand of power, and coming in the clouds of heaven.
14:63 Ndipo mkulu wa ansembe adang'amba malaya ake, nanena, Tifuniranjinso mboni zina?	14:63 Then the high priest rent his clothes, and saith, What need we any further witnesses?
14:64 Mwamva mwano wake; muyesa bwani? Ndipo onse adamsutsa Iye kuti ayenera kufa.	14:64 Ye have heard the blasphemy: what think ye? And they all condemned him to be guilty of death.
14:65 Ndipo ena adayamba kumthira malobvu Iye, ndi kuphimba nkhope yake, ndi kum'bwanyula, ndi kunena naye, Lota; ndipo atumikiwo adampana Iye khofi ndi manja awo.	14:65 And some began to spit on him, and to cover his face, and to buffet him, and to say unto him, Prophecy: and the servants did strike him with the palms of their hands.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
14:66 Ndipo pamene Petro adali pansi m'bwalo, anadzapo m'modzi wa adzakazi a mkulu wa ansembe;	14:66 And as Peter was beneath in the palace, there cometh one of the maids of the high priest:
14:67 Ndipo pamene adamuwona Petro alikuwotha moto, namuyang'ana iye, adanena, Iwenso udali naye Yesu ku Mnazarete.	14:67 And when she saw Peter warming himself, she looked upon him, and said, And thou also wast with Jesus of Nazareth.
14:68 Koma adakana, nanena, Sindimdziwa kapena kumvetsa chimene uchinena iwe; ndipo adatuluka kupita kuchipata; ndipo tambala adalira.	14:68 But he denied, saying, I know not, neither understand I what thou sayest. And he went out into the porch; and the cock crew.
14:69 Ndipo mdzakaziyo adamuwonanso iye, nayambanso kunena ndi iwo akuyimilirapo, Uyu ndi m'modzi wa iwo.	14:69 And a maid saw him again, and began to say to them that stood by, This is one of them.
14:70 Ndipo adakananso. Ndipo patapita mphindi, akuyimilirapo adanenanso ndi Petro, zowonadi uli wa awo; pakutinso uli Mgalileya. Pakuti ndi mayankhulidwe ako agwirizana ndi iwo.	14:70 And he denied it again. And a little after, they that stood by said again to Peter, Surely thou art one of them: for thou art a Galilaeen, and thy speech agreeth thereto.
14:71 Koma iye adayamba kutemberera, ndi kulumbira, ndikunena, Sindidziwa za munthuyu amene inu muyankhula za Iye.	14:71 But he began to curse and to swear, saying, I know not this man of whom ye speak.
14:72 Ndipo tambala adalira kachiwiri, Ndipo Petro adakumbukira umo Yesu adati kwa iye, kuti, Tambala asadalire kawiri udzandikana katatu. Ndipo poganizira ichi adalira misozi.	14:72 And the second time the cock crew. And Peter called to mind the word that Jesus said unto him, Before the cock crow twice, thou shalt deny me thrice. And when he thought thereon, he wept.
<b>Mark 15</b>	<b>Mark 15</b>
15:1 Ndipo pomwepo m'mawa adakhala upo ansembe akulu, ndi akulu a anthu, ndi alembi, ndi akulu a milandu onse, namanga Yesu, namtenga, nampereka kwa Pilato.	15:1 And straightway in the morning the chief priests held a consultation with the elders and scribes and the whole council, and bound Jesus, and carried him away, and delivered him to Pilate.
15:2 Ndipo Pilato adamfunsa Iye, Kodi ndiwe Mfumu ya Ayuda? Ndipo poyankha adati kwa iye, Mwatero ndinu.	15:2 And Pilate asked him, Art thou the King of the Jews? And he answering said unto them, Thou sayest it.
15:3 Ndipo ansembe akulu adamnenera Iye zinthu zambiri koma sadayakhe kanthu.	15:3 And the chief priests accused him of many things: but he answered nothing.
15:4 Ndipo Pilato adamfunsanso, nanena, Suyankha kanthu kodi? Tawona, akuchitira umboni Iwe mokutsutsa zinthu zambiri zotere.	15:4 And Pilate asked him again, saying, Answerest thou nothing? behold how many things they witness against thee.
15:5 Koma Yesu sadayankhenso kanthu; kotero Pilato adazizwa.	15:5 But Jesus yet answered nothing; so that Pilate marvelled.
15:6 Tsopano amkawamasulira paphwando wa mndende m'modzi, amene iwo adamfuna.	15:6 Now at that feast he released unto them one prisoner, whomsoever they desired.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
15:7 Ndipo adalipo wina dzina lake Baraba, womangidwa pamodzi ndi ena wopanduka, amene adapha munthu mumpanduko.	15:7 And there was one named Barabbas, which lay bound with them that had made insurrection with him, who had committed murder in the insurrection.
15:8 Ndipo khamu lidafuwuula niliyamba kupempha Iye kuti achite monga adali kuwachitira iwo.	15:8 And the multitude crying aloud began to desire him to do as he had ever done unto them.
15:9 Koma Pilato adawayankha iwo, nanena Kodi mufuna ndikumasulireni Mfumu ya Ayuda?	15:9 But Pilate answered them, saying, Will ye that I release unto you the King of the Jews?
15:10 Pakuti adazindikira kuti ansembe akulu adamperaka Iye mwa njiru.	15:10 For he knew that the chief priests had delivered him for envy.
15:11 Koma ansembe akulu adasonkhezera anthu, kuti makamaka awamasulire Baraba.	15:11 But the chief priests moved the people, that he should rather release Barabbas unto them.
15:12 Ndipo Pilato adayankha natinso kwa iwo, Pamenepo ndidzachita chiyani ndi Iye amene mumtchula Mfumu ya Ayuda?	15:12 And Pilate answered and said again unto them, What will ye then that I shall do unto him whom ye call the King of the Jews?
15:13 Ndipo adafuwulanso, Mpachikeni Iye.	15:13 And they cried out again, Crucify him.
15:14 Pamenepo Pilato adanena nawo, Chifukwa chiyani, Iye adachita choyipa chotani? Koma iwo adafuwulitsatu, Mpachikeni Iyeyo.	15:14 Then Pilate said unto them, Why, what evil hath he done? And they cried out the more exceedingly, Crucify him.
15:15 Ndipo Pilato pofuna kuwakhazikitsa mtima anthuwo, adawamasulira Baraba, namperaka Yesu, atamkwapula kuti akapachikidwe.	15:15 And so Pilate, willing to content the people, released Barabbas unto them, and delivered Jesus, when he had scourged him, to be crucified.
15:16 Ndipo asilikali adachoka naye nalowa m'bwalo, ndilo Pretoriyo; nasonkhanitsa gulu lawo lonse.	15:16 And the soldiers led him away into the hall, called Praetorium; and they call together the whole band.
15:17 Ndipo adambveka Iye chibakuwa, naluka korona wa minga, nambveka pa mutu pake.	15:17 And they clothed him with purple, and platted a crown of thorns, and put it about his head,
15:18 Ndipo adayamba kumulonjera Iye, nati, Tikuwoneni, Mfumu ya Ayuda!	15:18 And began to salute him, Hail, King of the Jews!
15:19 Ndipo adampana Iye pamutu pake ndi bango, namthira malobvu, nampindira mawondo, namlambira.	15:19 And they smote him on the head with a reed, and did spit upon him, and bowing their knees worshipped him.
15:20 Ndipo atatha kum'nyoza adambvula chibakuwacho nam'bveka Iye zobvala zake. Ndipo adatuluka naye kuti akampachike Iye.	15:20 And when they had mocked him, they took off the purple from him, and put his own clothes on him, and led him out to crucify him.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
15:21 Ndipo adamkangamiza wina, Simoni wa ku Kerene, amene amapitirirapo kuchokera kumudzi, atate wawo wa Alesandere ndi Rufu, kuti anyamule mtanda wake.	15:21 And they compel one Simon a Cyrenian, who passed by, coming out of the country, the father of Alexander and Rufus, to bear his cross.
15:22 Ndipo adamtenga kupita naye ku malo Gologota, ndiwo wosandulika, Malo achigaza.	15:22 And they bring him unto the place Golgotha, which is, being interpreted, The place of a skull.
15:23 Ndipo adampatsa vinyo wosanganiza ndi mure; koma Iye sadamlandire	15:23 And they gave him to drink wine mingled with myrrh: but he received it not.
15:24 Ndipo pamene adampachika Iye, adagawana zobvala zake, ndi kuchita mayere pa izo, kuti adziwe yense adzatenga chiyani.	15:24 And when they had crucified him, they parted his garments, casting lots upon them, what every man should take.
15:25 Ndipo lidali ora lachitatu ndipo iwo adampachika Iye.	15:25 And it was the third hour, and they crucified him.
15:26 Ndipo lembo la mlandu wake lidalembedwa pamwamba, MFUMU YA AYUDA.	15:26 And the superscription of his accusation was written over, The King Of The Jews.
15:27 Ndipo adampachika pamodzi ndi achifwamba awiri; m’modzi kudzanja lake lamanja ndi wina kulamazere.	15:27 And with him they crucify two thieves; the one on his right hand, and the other on his left.
15:28 Ndipo malemba adakwaniritsidwa, amene adati, Ndipo adawerengedwa pamodzi ndi omphwanya malamulo.	15:28 And the scripture was fulfilled, which saith, And he was numbered with the transgressors.
15:29 Ndipo iwo wodutsapo adamchitira Iye mwano, napukusa mitu yawo nanena, Ha! Iwe wopasula kachisi ndi kum’ manga masiku atatu,	15:29 And they that passed by railed on him, wagging their heads, and saying, Ah, thou that destroyest the temple, and buildest it in three days,
15:30 Udzipulumutse wekha, nutsike pamtandapo.	15:30 Save thyself, and come down from the cross.
15:31 Moteronso ansembe akulu adamtoza mwa iwo wokha pamodzi ndi alembi’nanena, Adapulumutsa ena; Iye yekha sakhoza kudzipulumutsa.	15:31 Likewise also the chief priests mocking said among themselves with the scribes, He saved others; himself he cannot save.
15:32 Atsike tsopano pamtanda, Khristu Mfumu ya Israyeli, kuti tiwone ndipo tikhulupirire. Ndipo iwo wopachikidwa naye adamlalatira.	15:32 Let Christ the King of Israel descend now from the cross, that we may see and believe. And they that were crucified with him reviled him.
15:33 Ndipo pofika ola la chisanu ndi limodzi, padali mdima padziko lonse, kufikira ola la chisanu ndi chinayi.	15:33 And when the sixth hour was come, there was darkness over the whole land until the ninth hour.
15:34 Ndipo pa ola la chisanu ndi chinayi Yesu adafuwula ndi mawu wokweza, Eloi, Eloi, lamasabakitani? Ndiko kutathauza, Mulungu wanga Mulungu wanga mwandisiyiranji Ine?	15:34 And at the ninth hour Jesus cried with a loud voice, saying, Eloi, Eloi, lama sabachthani? which is, being interpreted, My God, my God, why hast thou forsaken me?

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
15:35 Ndipo ena woyimilirapo, pakumva adanena, Taonani akuyitana Eliya.	15:35 And some of them that stood by, when they heard it, said, Behold, he calleth Elias.
15:36 Ndipo adathamanga wina, nadzaza chinkhupule ndi vinyo wosasa, nachiyika pa bango, nampatsa kuti amwe, nanena, Mulekeni; tiwone ngati Eliya adza kudzamtsitsa.	15:36 And one ran and filled a sponge full of vinegar, and put it on a reed, and gave him to drink, saying, Let alone; let us see whether Elias will come to take him down.
15:37 Ndipo Yesu adafuula mokwezetsa mawu, napereka Mzimu wake.	15:37 And Jesus cried with a loud voice, and gave up the ghost.
15:38 Ndipo chinsalu chotchinga cha m'kachisi chidang'ambika pakati, kuyambira kumwamba kufikira pansu.	15:38 And the veil of the temple was rent in twain from the top to the bottom.
15:39 Ndipo pamene Kenturiyo, woyimilirapo popenyana ndi Iye, adawona kuti adapereka Mzimu koteru, adati, Zowonadi, munthu uyu adali Mwana wa Mulungu.	15:39 And when the centurion, which stood over against him, saw that he so cried out, and gave up the ghost, he said, Truly this man was the Son of God.
15:40 Ndipo adaliponso pamenepo akazi akuyang'anira patali; mwa iwo padali Mariya wa Magadala ndi Mariya amake wa Yakobo wam'ng'ono ndi wa Yose, ndi Salome.	15:40 There were also women looking on afar off: among whom was Mary Magdalene, and Mary the mother of James the less and of Joses, and Salome;
15:41 (Amene adamsata Iye, pamene adali mu Galileya, namtumikira Iye;) ndi akazi ena ambiri, amene adakwera kudza ndi Iye ku Yerusalemu.	15:41 (Who also, when he was in Galilee, followed him, and ministered unto him;) and many other women which came up with him unto Jerusalem.
15:42 Ndipo tsono atafika madzulo, popeza mpa tsiku lokonzekera, ndilo la pambuyo pa sabata.	15:42 And now when the even was come, because it was the preparation, that is, the day before the sabbath,
15:43 Adadzapo Yosefe wa ku Arimateya, mkulu wa milandu wotchuka, amene yekha adali kuyembekezera Ufumu wa Mulungu; nalimba mtima kwa Pilato, napempha mtembo wa Yesu.	15:43 Joseph of Arimathaea, an honourable counsellor, which also waited for the kingdom of God, came, and went in boldly unto Pilate, and craved the body of Jesus.
15:44 Ndipo Pilato adazizwa ngati adamwaliradi; nayitana Kenturiyo, namfunsa ngati adamwalira kale.	15:44 And Pilate marvelled if he were already dead: and calling unto him the centurion, he asked him whether he had been any while dead.
15:45 Ndipo pamene adachidziwa ndi Kenturiyo, adampatsa Yosefe mtembowo.	15:45 And when he knew it of the centurion, he gave the body to Joseph.
15:46 Ndipo adagula bafuta, namtsitsa Iye, namkulunga m'bafutamo, namuyika m'manda wosemedwa m'thantwe; nakunkhunizira mwala pa khomo la manda.	15:46 And he bought fine linen, and took him down, and wrapped him in the linen, and laid him in a sepulchre which was hewn out of a rock, and rolled a stone unto the door of the sepulchre.
15:47 Ndipo Mariya wa Magadala ndi Mariya amake a Yosefe adapenya pomwe adayikidwapo	15:47 And Mary Magdalene and Mary the mother of Joses beheld where he was laid.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
<b>Mark 16</b>	<b>Mark 16</b>
16:1 Ndipo litapita sabata, Mariya wa Magadala, ndi Mariya amake wa Yakobo, ndi Salome, adagula zonunkhira, kuti akadze kumdzodza Iye.	16:1 And when the sabbath was past, Mary Magdalene, and Mary the mother of James, and Salome, had bought sweet spices, that they might come and anoint him.
16:2 Ndipo anadza kumanda m`mawa tsiku loyamba la Sabata, litatuluka dzuwa.	16:2 And very early in the morning the first day of the week, they came unto the sepulchre at the rising of the sun.
16:3 Ndipo adalikunena mwa wokha, Adzaticunkhunizira ndani mwalawo, pakhomola manda?	16:3 And they said among themselves, Who shall roll us away the stone from the door of the sepulchre?
16:4 Ndipo pamene adakweza maso adawona kuti mwala wakunkhunizidwa, pakuti udali waukulu ndithu.	16:4 And when they looked, they saw that the stone was rolled away: for it was very great.
16:5 Ndipo pamene adalowa m`manda, adawona m`nyamata atakhala kumbali ya ku dzanja lamanja, wobvala mwinjiro woyera; ndipo iwo Adachita mantha.	16:5 And entering into the sepulchre, they saw a young man sitting on the right side, clothed in a long white garment; and they were affrighted.
16:6 Ndipo iye adanena nawo, musaope: Muli kufuna Yesu Mnazarete amene adapachikidwa; adawuka; Sali pano; tawonani, mbuto m`mene adayikamo Iye.	16:6 And he saith unto them, Be not affrighted: Ye seek Jesus of Nazareth, which was crucified: he is risen; he is not here: behold the place where they laid him.
16:7 Koma mukani uzani wophunzira ake, ndi Petro, kuti akutsogolereni inu ku Galileya; kumeneko mudzamuwona Iye, monga adanena ndi inu.	16:7 But go your way, tell his disciples and Peter that he goeth before you into Galilee: there shall ye see him, as he said unto you.
16:8 Ndipo adatuluka mwamsanga, nathawa kumanda; pakuti kunthunthumira ndipo anadabwa; ndipo sadawuze kanthu munthu aliyense; pakuti adachita mantha.	16:8 And they went out quickly, and fled from the sepulchre; for they trembled and were amazed: neither said they any thing to any man; for they were afraid.
16:9 Ndipo pamene Yesu adawuka mamawa tsiku loyamba la sabata, adayamba kuwonekera kwa Mariya wa Magadala, amene adamtulutsa ziwanda zisanu ndi ziwiri.	16:9 Now when Jesus was risen early the first day of the week, he appeared first to Mary Magdalene, out of whom he had cast seven devils.
16:10 Ndipo Iye adapita kukawauza iwo amene amakhala naye, ali ndi chisoni ndipo kungolira.	16:10 And she went and told them that had been with him, as they mourned and wept.
16:11 Ndipo iwowo, pamene adamva kuti ali ndi moyo, ndi kuti adawonekera kwa iye, sadakhulupirire.	16:11 And they, when they had heard that he was alive, and had been seen of her, believed not.
16:12 Ndipo zitatha izi; adawonekeranso iye m`mawonekedwe ena kwa awiri a iwo amene anali kupita kumudzi.	16:12 After that he appeared in another form unto two of them, as they walked, and went into the country.

NYANJA	NEW INTERNATIONAL VERSION
16:13 Ndipo iwowa adachoka nawauza wotsala; koma palibe amene adakhulupirira iwo.	16:13 And they went and told it unto the residue: neither believed they them.
16:14 Ndipo chitatha icho adawonekera kwa khumi ndi m;modzi, alikuseyama pachakudya; ndipo adawadzudzula chifukwa cha kusakhulupirira kwawo ndi kuwumitsa mtima, popeza sadakhulupirira iwo amene adamuwona, atawuka Iye.	16:14 Afterward he appeared unto the eleven as they sat at meat, and upbraided them with their unbelief and hardness of heart, because they believed not them which had seen him after he was risen.
16:15 Ndipo adanena nawo, Mukani ku dziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa wolengedwa onse.	16:15 And he said unto them, Go ye into all the world, and preach the gospel to every creature.
16:16 Amene akhulupilira nabatizidwa, adzapulumuka; koma amene sakhulupirira adzalangidwa.	16:16 He that believeth and is baptized shall be saved; but he that believeth not shall be damned.
16:17 Ndipo zizindikiro izi zidzawatsata iwo akukhulupilira; m'dzina langa adzatulutsa ziwanda, adzayankhula ndi malilime atsopano;	16:17 And these signs shall follow them that believe; In my name shall they cast out devils; they shall speak with new tongues;
16:18 Adzatola njoka ndipo ngakhale akamwa kanthu kakufa nako, sikadzawapweteka; adzayika manja awo pa wodwala, ndipo adzachira.	16:18 They shall take up serpents; and if they drink any deadly thing, it shall not hurt them; they shall lay hands on the sick, and they shall recover.
16:19 Pamenepo Ambuye, atatha kuyankhula nawo, adalandiridwa Kumwamba, nakhala pa dzanja la manja la Mulungu.	16:19 So then after the Lord had spoken unto them, he was received up into heaven, and sat on the right hand of God.
16:20 Ndipo iwowa adatuluka, nalalikira ponseponse, ndipo Ambuye adagwira ntchito nawo pamodzi, natsimikiza mawu ndi zizindikiro zakutsatapo. Amen.	16:20 And they went forth, and preached every where, the Lord working with them, and confirming the word with signs following. Amen.